


MAFUNSO NDI MAYANKHO

AHEBRI, GAWO II

 Ine ndikufuna poyamba kuti ndikuthokozeni aliyense wa inu omwe munalandira uthenga “kuti mumupempherere mkazanga.” Iye anali atadwalika, kwambirimbiri. Ife sitimadziwa chomwe icho chinali, ndipo sitikudziwa chomwe chinachitika, kungangokhala kusanza kopitirira ndipo iye anali chikomokere mochitika, ndi malungo pafupi handiredi n faifi, timachita kumamukulunga iye mu mabulangeti a ayesi. Chotero . . .koma iye ali bwino bwino tsopano. Malungo onse awo atha, ndipo iye alibwino. Kotero iye wafooka kwambiri, wataya pafupi mapaundi khumi, ine ndikulingalira. Iye sana . . . Usikuuno iye anameza chakudya chake choyamba kuchokera Lamlungu. Ndipo chotero iye wakhala ali akudwala kwambiri, ndipo ife tinadalira Ambuye pa iye, ndipo Iye angomudutsitsa iye kumene. Tsopano ife tikufuna kuti tikuuzeni inu kuti mupitirize kupemphera kuti iye apezenso mphamvu zake.

³⁰⁴ Ndipo tsopano, sabata ikubwera iyi, Ambuye akalola, ine ndiyenera kuti ndipite ku Miami. Mzanga wachikulire, M’bale Bosworth, akupita Kwawo, ndipo iye ali pafupi usinkhu wa zaka zana tsopano. Ndipo iye anandiitana ine, iye anati, “M’bale Branham, bwera udzandiwone ine pomwe pano, ine ndikufuna kuti ndikuuze iwe chinachake ine ndisanapite.” Ndipo iye . . . Chabwino, ine ndikuganiza iye akufuna kuti akandipempherere ine, ndi kungosanjika manja ake pa ine asanachoke, inu mukudziwa.

³⁰⁵ Ndipo i—ine ndikuyembekeza kuti ine ndikhoza kutsirizitsa masiku anga ndi ulemu wonga wa F.F. Bosworth. Mwa anthu onse omwe ine ndikuwadziwa mdziko, munthu aliyense yemwe ine ndakomanapo naye mu dziko, ine sindinayambe ndakomanapo ndi munthu yemwe ine ndinakhumba chotero kuti ndikhale monga iye, monga F.F. Bosworth; n—ngati mtumiki, chomwe ine ndikutanthauza. Ine sindinayambe ndamumvapo munthu mmodzi, mdziko-lonse, kulikonse, anayankhulapo chinthu chimodzi za F.F. Bosworth koma zomwe zinali ndendende basi chirichonse “Mkhristu,” ndi chirichonse “m’bale weniweni.”

³⁰⁶ Posiyana timasiya mmbuyo mwathu mopanda mapazi pa mchenga wa nthawi. Iye ndi m’bale wodabwitsa, ndipo iye wakalamba kwenikweni tsopano, pafupi handiredi. Kotero iye ali—akungopita Kwawo, ndizo zonse, ndipo iye anandiuza ine. Iye amadziwa kuti iye akupita, ndipo anali akungoyembekezera. Iye anati nthawi yokoma ya moyo wake ndi pakali pano pamene

iyе akungoyembekezera, koma anati iye akudziwa kuti iye anali kupita.

307 Ine ndinati, “Ine ndikuyenera kuti ndipite ku Michigan sabata ino, M’bale Bosworth.”

308 Ndipo iye anati, “Chabwino, usati ukakhale motalika kwambiri, M’bale Branham, ine sindingakhoze kukhalapo nthawi yotalikirapo kwambiri. Ine ndikukhala wofookera nthawi inayonse.”

309 Kotero iye wakhala mochuluka kwambiri mzanga kwa ine, kuti ndisapite uko. Tsopano, ngati ine nditi ndiwuluke popita uko, i—ine ndidzawuluka pobwerera ndipo mwina kudzakhala nditabwerera mwina pofika Lamlungu usiku; ngati sichoncho, chabwino, ndiye ine ndidzayenera kuti ndidzayende pa galimoto, ndipo izo zikhoza kunditengera ine motalikirira pang’ono.

310 Ndipo zimupemphererani M’bale Bosworth. Zingopempherani kuti Mulungu...ndipo pamene Iye azimutenga mbadwa yachikulireyo, kuti Iye adzangotumiza galeta wamoto ndi kudzamunyamula iye, mwaona. Ine ndimamukonda iye, iye ali ngati bambo kwa ine.

311 Bambo wina wachikulire...iye ndi m’bale Seward. I—ine ndimakhala ngati wokondera kwa anthu achikulire, i—ine ndimawakonda iwo. Ndipo M’bale Seward wachikulire, iye anapita kokagona monga chomwecho, nayenso. Zoono, M’bale Seward sanali wachikulire kwenikweni, ine sindikuganiza, monga M’bale Bosworth.

312 Ndipo zimupemphererani M’bale Bosworth. Chirichonse sichiri mwamaluwa kuzungulira pa malopo, koma n—n...Iye akusowa mapemphero anu, koma osati mochuluka mopanda kanthu koma basi ake...kuti Mulungu amulole iye apite mwa mtendere.

313 Tsopano...Ndiyeno ife tikufuna kuti tikumbukire, naponso, kuti mawa, Ambuye akalola, ife timuika mmodzi wa amzathu wochokera ku mpingo uno, M’bale Sol Coates. Iye wakhala ali kuno nthawi zingapo, amagwira ntchito mu positi ofesi kwa zaka. Ndipo iye anakafera ku chipatala cha Maveterani usiku wina. M’bale Cox ndi ine tinapita uko kukamuwona iye, ndipo iye anali...motsika kwambiri. Ndipo iye watsogola tsopano, Mkhristu. Ndipo ife ndi oti tikamuike iye ku Coot—nyumba yamaliro ya a Coot mawa madzulo wani koloko, M’bale Neville ndi ine. Oyimba atatu a Neville adzakakhala akuimba; ndipo ife tidzakhala tikugawana utumiki, M’bale Neville ndi ine. Ndi izo, ine sindimadziwa pamene ife timakonza dongosololo basi kuti chiani, ndi chifukwa cha Meda. Ndipo kotero, ndiye, maliro ake akhala mawa madzulo wani koloko, kunyumba yamaliro ya a Coot.

314 Ndiyeno, thuu koloko, Lachisanu, Bambo Wheller. Ife timamutcha iye Pod Wheeler; iye ali, ine ndaiwala kwenikweni lomwe liri lake lolondola...Ndipo, inu mukudziwa, i—ine ndinangoziwona izo mu pepala ndipo ine sindimadziwa yemwe iye anali, mpaka ine nditafunsa. Iye anali woyandikana nafe kwa zaka, n—ndipo iye wangomwalira kumene. Iye anali komwe kuno patsogolopa mu mpingo, usiku wina, ndipo ine ndimayesera kuti ndimufikitse iye pomabwera ku tchalitchi. Usiku wina, pafupi masabata atatu apitawo, ndinaima apo pomwe, ndipo ine ndinkangoyesera kuti ndimukakamize iye kuti azibwera ku tchalitchi. Chifukwa, ine sindikuganiza kuti ankapita ku tchalitchi kapena anali ndi ntchito ya mtundu wina uliwonse, komabe iye ali ndi mnyamata yemwe ali mlaliki wa Chibaptisti. Koma iye analibe ntchito yoidziwa iliyonse monga momwe ine ndikudziwira, ndipo iye watsogola tsopano kukakomana ndi Mulungu. Koteru izo zidzakhala Lachisanu madzulo thuu koloko ku nyumba yamaliro ya a Coot. Ndiponso, M'bale Neville ndi iwo adzakhala akuimba, ndi pa maliro awo uko.

315 Ndipo chotero, ngati aliyense wa inu yemwe akufuna kuti akakhale nawo pa mautumikiwo, ndi mawa pa 2:00...kapena mawa pa 1:00. Ine ndikuganiza ndiko kulondola. Sichoncho izo, m'bale? Ndi 2:00, enawo. Nkulondola uko? 2:00 Ku nyumba yamaliro ya a Coot.

316 Ndipo tsopano, Lamlungu mmawa...Loweruka padzakhala kulengeza. Ndipo M'bale Neville mwinamwake adzakudziwitsani inu, apo, chomwe chiri...ngati ife tingakhoze kukhala ndi msonkhano wa machiritso Lamlungu usiku, kapena nthawi yomwe ife tidzakhale titabwerera ngati ine nditi ndidzawuluke popita k—ku Florida kukamuwona M'bale Bosworth. Ine sindikudziwa basi kuti ndikachoka chotani kwa iye, iye ndi bwenzi lakale lokonedwa chotero. Ndipo mwinamwake nkukomana kwathu kotsiriza, ngati Ambuye ati aroleze izo, pa dziko lapansi pano. Ndipo iye...ine sindikudziwa ngati nditi ndikachoke kwa iye nthawi yomweyo kapena ayi; ndipo ine sindikufuna kukachoka kwa iye, koma, inu mukudziwa momwe izo ziliri, iwe umakhala ndi zinthu zina zomwe iwe umayenera kuti ukazichite.

317 Tsopano pali neno limodzi lomwe ine ndikufuna kuti ndilinine pano pamene palibe ochuluka kwambiri, ndi anthu omwe ali abwenzi anga.

318 Ndine wokondwa kumuwona Mlongo Smith apo. Nthawi yoyamba yomwe ine ndamuwona iye pa nthawi yaitali. Muli bwanji inu Mlongo Smith? Chaka, mai, ine ndikukhulupirira nthawi yotsiriza yomwe ine ndinakuwonani inu...[Mlongo Smith akuyankhula—Mkonzi.] Ku Benton Harbor, ine ndikuyembekeza kudzakafika uko nthawiyina. Izo nzabwino. Ine ndikukhulupirira nthawi yotsiriza yomwe ine ndinakuwonani inu, panali pa mwambo wa maliro mu

Louisville. Ndipo ine ndikumukumbukira Mlongo Smith mwabwino kwambiri. Momwe ife. . .Ine ndinkakonda kubwera ndi kudzamutenga iye mu bokosibode pamene ife timapita ku tchalitchi. Phula lakale la makala litakanirira kumbuyo kwakeko ndi zotchingira zikukupizira mmwamba ndi pansi, ndi kukuzizira; ndipo ine, phazi limodzi litaponda panja. O, mai. Madzi ochuluka adutsa pansi pa mtsinjewu kuchokera pajapa, Mlongo Smith. Inde, bwana. Chabwino, ife tikuwathokoza Ambuye chifukwa cha zikumbutso zofunika izo, ndipo tidakamakondabe Iye.

³¹⁹ Chinthu chimodzi, winawake akhoza kudabwa, usiku wina. . .Ine ndinali kuyankhula ndi M'bale Fleeman kunja uko pa msewu. Ndipo nthawizina wina anati, “Mwamsanga msonkhano ukangotha, nchiani chimamupangitsa M'bale Branham kuuyamba ndi kumapita?”

³²⁰ Ichi ndi chomwe chiri, mkazi wanga amakhala ali yekha. Mwaona? Ndipo ngati ine ndiyamba kuyankhula, ine ndimayankhula theka la usiku, ndipo uko iye ali, atakhala uko mwayekha nthawi zambiri. Ndipo nchifukwa chake ine ndimafulumira kutuluka, kuti ndikafike kwa iye, inu mukuona, nthawi yausiku; chifukwa ine ndikayamba kuyankhula, ine ndimayankhula motalikitsa kwambiri. Ine ndimayankhula ndi *uyu* theka la ora. Ine sindingakhoze kungodutsa apo nkuti, “Muli bwanji *inu* usikuuno? *Inu* muli bwanji? *Inu* muli bwanji?” Ine sindimachita zimenezo. Ine ndimangoima ndi kuyamba kuyankhula; ndipo wina akayamba kuyankhula za chinachake, ndiyeno ine ndimakhala pamenepo kwa ora. Mwaona? Ndipo nchifukwa chake, iye amakhala akudikira ndi zina zotero. Ndicho chifukwa chake izo ziri. Ine sindimafuna basi kuti inu muziganiza kuti izo zinali chifukwa chakuti ine sindimafuna kuti ndizikomana ndi amzanga ndi kugwirana chanza nawo, ndi kufotokoza chijanano chatu ndi zina zotero, koma iyo yangokhala nkhami ya mtundu umenewo.

³²¹ Kotero, tsopano, aliyense akhale mu pemphero kwa odwala ndi osautsika.

³²² Ndipo Akazi a Harvey ali mu vuto lonse ilo, iwo akupeza bwino. Inde, bwana. Ndipo ine sindikuwona. . .I. . .Tsopano pakhoza kukhala pali, momwe ine ndikudziwira, winawake, dokotala pano. Ndipo ngati ine ndikulakwitsa pa nsanja ino, Mulungu andikhululukire ine. Koma ine ndikukhulupirira Mulungu adzafuna madotolo awo adzayankhire pa zomwe iwo achita kwa mkaziyo. I—ine ndimakhulupirira mu opareshoni, ine ndimawakhulupirira mankhwala. Ndithudi, ine ndimakhulupirira izo. Ine ndikuganiza Mulungu anawatumiza iwo kuno kuti azitithandiza ife, basi monga Iye anatomizira amakaniko a magalimoto ndi zina zotero. Koma mkazi wamng'ono uyo, dokotala anamugoneka iye chagada, ndipo

anati, “Iye anali atadzazidwa ndi khansa, palibe kanthu komwe kanachitidwa.” Mayi wamng’ono ali ndi gulu la ana.

³²³ Ine ndinapita uko kwa iye, ndipo ndinakayesera kukawafotokozerwa iwo momwe kuti kupyolera mu pemphero . . . N—ndipo iye wangokhala mkazi wamng’ono, pafupi twente-faifi. Ndi momwe Mulungu anamuchizira mwana wake wamng’ono, iye akutchedwa “mwana wa chozizwitsa” ali ku chipatala chawana tsopano, ndi menjaitisi. Ndipo chikhalidwe choipa chakecho cha—munthu wamng’ono momwe analiri, ndipo Ambuye anamuchiza iye basi nthawi yomweyo. Iwo, madotolo, samakhoza kuzimvetsa izo. Ine ndinapita uko kwa Akazi a Harvey, ndipo ine ndinati, “Tsopano, Akazi a Harvey, madotolo akulepherani inu?”

³²⁴ “Inde, bwana. Ndizo . . .”

³²⁵ Ndipo amuna awo anati, “Inde, palibe chinthu chimene chingakhoze kuchitidwa, iye wangodzaza kwathunthu ndi khansa.”

³²⁶ Ine ndinati, “Chabwino, tsopano chimene ife tikuti tichite, ndi kukhulupirira Mulungu, kuti Mulungu—achiza . . . akuchizani inu.” Ndipo ine ndinati, “Momwe zingachitikire, khansa ikhoza kusachoka mwamsanga; koma ngati ife tipemphera, ndiye moyo wa khansawo uchoka. Inu mukhoza kukhala mukudwalabe kwa kanthawi apobe, n—ndipo” ine ndinati “inu mukhoza kupeza bwinopo nthawi yomweyo.” Ndipo ine ndinati, “Ndiye pakatha masiku angapo inu mukhoza kudwalirapo kuposa kale.” Koma ine ndinati, “Inu muyenera kuti muike chikhulupiriro chanu moitsutsa khansayo.” Ine ndinati, “Ngati khansayo ikhalabe moyo, inu mufa. Ngati khansayo ifa, inu mukhala moyo.” Ndipo ine ndinati, “Tsopano ife tikupemphera.”

³²⁷ Ndipo ife tinapemphera, ndipo ndi umboni uliwonse womwe ine ndinawuona, Mulungu analikhudza thupi la mkaziyo. Ndipo mwamsanga iye anapeza bwinoko, iye anapita mpaka kukawawona amayi anga, iye anawachezera oyandikana nawo, (pamene iye anali momvetsa chisoni chotero) analibe kupweteka kulikonse. Ndiyeno atatha pafupi masiku atatu iye anayamba kumadwala kachiwiri.

³²⁸ Ndiyeno ndinadzapeza kuti mzinda unati iwo “ulipira mtengo wa dotolo, ngati madotolo atamuchita oparesoni iye.”

³²⁹ Ndipo tsopano ngati ine ndikulakwitsa, Mulungu andikhululukire ine. Koma iwo anamutenga mayi wamng’ono uyo, munamupanga “mbira yoyeserera” pa iye. Iwo anamutengera iye uko, ndipo anachotsa ngakhale matumbo ake kuchokera mmimba mwake, ndi chirichonse. Anatenga zonse kuchokera ku chikodzodzo ndi kuchokera mu matumbo, ndi kuzitulutsira izo pambali. Ndipo anali pa tebulo ya oparesoni maora naini ndi chinachake. Namwino anati, “Apo

pankawoneka ngati khola lopheramo nyama, pamene iwo ankaponyera zamkati zake kuchokera malo kupita pa malo, ndi kuika mazira a pulasitiki ndi machubu a pulasitiki.” Izo ndi mosabisa, koma ndi zoona. Ndi matumbo a pulasitiki ndi zinthu monga chomwecho, ndi kumusiya mkaziyo ali mu ululu uwo, mayi wamng’ono. Ine ndikuti, mwa njira yanga yoganizira izo, madokotala amenewo ali ndi mulandu wa kupha.

³³⁰ Iye anawauza iwo, iye anati, “M’bale Branham anandipempherera ine.” Ndipo anati, “Ife tikuti tizikhulupirira kuti khansa yathu. . .kuti khansayo yafa.”

³³¹ Anati, “Ine ndiri ndi nkhani ina kwa inu, ‘Khansa yanu ili moyo.’”

³³² Iye akanadziwa bwanji izo? Iyo inali mkati mwake, palibe X re yomwe ingakhoze kuzidziwa izo. Khansa. . . Inu simungakhoze kuidziwa khansa ndi X re, iyo ndi mnofu payokha, inu simungakhoze kuiwona iyo. Pali chinthu chimodzi chokha choti muchite, nkumukhapha mkaziyo ndi kumudula iye mzidutswa. Ndizo zonse. Tsopano ngati iye akanakhala mayi wamng’ono, ine ndikanangomulola iye kuti ayese chikhulupiriro chake kwa Mulungu malo momupanga “mbira yoyesererapo” pa winawake monga choncho. Tsopano ngati i—ngati ine ndikulakwitsa, ngati i—ine ndiri ndi zolinga zolakwika, ine ndikufuna Mulungu kuti andikhululukire ine, inu mukuona. Pakuti ine sindikufuna kuti inu muziganiza kuti ine sindimakhulupirira maoparesoni kapena sindimawakhulupira madotolo ndi zinthu. Izo zonse nzabwino. Koma ine ndikuganiza iwe umayenera kuti uzidziwa zomwe ukuzichita iwe usanakumbe mwa munthu, osati pa kungowagwiritsa iwo ntchito ngati zoyesererapo monga choncho. Ndiko kulondola. Ndipo tsopano, ndithudi, iye sakhoza kukhala moyo. Ndizo zonse. Ngati iye ati akhale moyo, izo ndithudi zikhala ziri chimodzi cha zozizwitsa zazikulu zomwe zinayamba zachitikapo. Pamene mkaziyo anayang’ana apo nawona kuti matumbo ake ali ku mbali imodzi, ndi impyzo zake zikugwirira ntchito kumbali ina, iye anangofa *choncho*, anafa. . .Bwanji, icho sichinali chinthu. . .kamunthu kakang’ono kosaukako kanali katapita. Iye ndi pafupi mayi wausinkhu wa zaka twente-thuu kapena twente-faifi zokha wa ana atatu kapena anai oti awalere. Chinthu chachisoni kwambiri chomwe ine ndinayamba ndachimvapo mu moyo wanga. Ine ndinati, “Mwa njira yanga yoganizira, dotoloyo ndi wolakwa pa. . .Ngati iye anamutenga mkazi uyo kuti akangoyesererapo chifukwa mzinda ukanati ulipirire izo, ndiye uko ndi kulakwa, zisamati zizilolezedwa.”

³³³ [Bambo akufunsa ngati Mulungu angamubwezeretse mkaziyo—Mkonzi.] Chabwino, ine ndikuuzani inu, m’bale, i—izo si zosatheka. Ndipo i—izo si. . .N—ndi zotheka, ndiponso mwinamwake. Chifukwa ine ndikumudziwa bambo yemwe

nkono wake unadulidwa, mu California (nonse mukuzitsatira izo nokha mu mapepala), anapemphereredwa, ndipo nkono *uwu* unaduka *apa*, wamela mpaka zala zikumela pa iwo tsopano; kudutsa pa chigongono, kudutsa polumikizira dzanja, kudutsa pa dzanja, ndi zigawo zopindila zala zinali zitabwerera pa zala, inu mukuona. Izo ziri mu, ine ndikukhulupira, *Herald of Faith* mwezi uliwonse. Ngakhale pamene atulutsa manja ake monga *chonchi*; asonyeza izo pamene nkono wake unadukira, pamene iwo wamerela. Mwezi uliwonse momwe iwo umamerela, kwa pafupi chaka.

334 [Bambo akuyankhula kuchokera mwa omvetsera kachiwiri—Mkonzi.] Zedi, uko nkulondola. Ine ndikukhulupirira. . . N—n—ndi chinthu chosowa, mwaona, ndi chinthu chosowa kwambiri. Kamodzi mu kanthawi ine ndazimvapo izo. Tsopano, ndi M'bale Bosworth, iye anamupempherera mkazi usiku wina. Ndipo ine ndinali naye mmodzi mu msonkhano wanga. Koma za M'bale Bosworth inali nthawi yomweyo; langa linatenga kanthawi pang'ono kuti ilo lichite izo.

335 Iye anamupempherera mkazi. . . Tsopano, ine ndinauwerenga umboni wa mkaziyo. Anali ndi khansa, alibe mphuno; inali itadyapo mphuno yakeyo. Ndipo mmawa wotsatira mkaziyo anali ndi mphuno. Tsopano, ine ndikudziwa izi. . . Tsopano, izo ndi za M'bale Bosworth, mu bukhu lake lotchedwa *Khristu Mchiritsi*, ine ndikukhulupirira, kapena, *Wobweretsa Chisangalalo*, limodzi lake. Tsopano, izo ziri mu umboni wa mkaziyo, pali dzina lake ndi adiresi. Ndipo iye ali ndi oyandikana nawo ndi madokotala ndi china chirichonse omwe atsimikizire izo, kuti izo zinachitika.

336 Tsopano, ku Little Rock, Arkansas, usiku wina mu chipinda, ine ndinapemphera uko. . . osati Little Rock, koma Jonesboro. Kuti ine ndinali nditapemphera. . . Ine ndinati, “Ine ndikhalapobe mpaka ine nditamupempherera munthu wotsiriza.” Ine ndinali masiku asanu ndi atatu ndi usiku pa nsanja, mwaona. Ndiyeno. . . ndipo mchipindamo munali mkazi anabweramo, anali atanyamula mpango wake mmwamba monga *chonchi*, ndipo ine ndinkaganiza kuti iye anali akulira. Ndipo ine ndinati. . . O, ine ndikuganiza inali thuu kapena firii koloko mmawa, ine ndinati, “Musalire, mlongo, Mulungu ndi mchiritsi.”

337 Iye anati, “Ine sindikulira, M'bale Branham.” Iye anauchotsa iwo; iye analibe mphuno, mwaona. Madokotala anali atanena. . . Khansayo inali itadya mpaka ku fupa loyera mwa iye. . . ilo linali kuonekera. Ndipo ine ndinali ndipemphero pa iye, ndipo ndinawafunsa Ambuye kuti amuchize iye.

338 Ndipo pafupi masabata anai kapena asanu kuyambira apo, ine ndinali mu Texarkana. Ndipo uko kunali njonda yovala

bwino itakhala apo, iye anati, “Kodi ine ndingangokhala ndi mawu amodzi nanu, M’bale Branham?”

339 Mwamsanga pamene iye anawuka pa nsanjayo, mmodzi wa othandizira anayesera kuti amukhalitse iye chete. Ine ndinati, “Chabwino, tiyeni tiwone.”

340 Iye anati, “Inu mukumuzindikira dona wamng’ono uyu?”

341 Ine ndinati, “Ayi, sindiri.”

342 Iye anati, “Ngati inu muyang’ana pa chithunzi ichi inu muchizindikira icho.” Ndipo iye anali wonyonga k—ku Texarkana, ndipo awo anali amayi ake ali ndi mphuno yatsopano itaphuka apo, itangowumbidwa monga inayo.

343 Tsopano izo zikusonyeza kuti Mulungu . . . Ine ndaziwonapo izo zitachitidwa. Tsopano, Mulungu akhoza kuchitira izo kwa Akazi a Harvey. Ndipo ine ndikupemphera kuti Iye achite, kwa kanthu kakang’ono kosauka kakufuna kukhala moyo.

344 M’bale Tony, kodi inu munali ndi chinachake? [M’bale Tony akunena za machiritso—Mkonzi.] Uko nkulondola. Ameni. Ameni. Inde, izo ndi zabwino, aponso. Inde, Iye ndithudi angachite izo, Iye ndi mchiritsi.

345 [Bambo wina akuchitira ndemanga—Mkonzi.] Inde. Inde. Inde, m’bale. Ameni. Zedi. Eya. Ine ndikutsimikiza . . . Ndipo ine ndikuyembekeza kuti Mulungu abwezeretsa icho kwa iwe, mwananga, iwe ukhoza kuchitenga kubwerera nachonso ndi kukamusonyeza iye. Ndizo ndendende basi. Izo ndi mwa umboni kwa ulemero wa Mulungu, pemphera kuti Mulungu achite izo. O, I—Iye . . . Ngati Iye ndi Mulungu Wamphamvuzonse, Iye akhoza kuchita zinthu zonse. Ngati Iye sangakhoze kuchita izo, zinthu zonse, Iye si Mulungu Wamphamvuzonse.

346 Pali chinachake chomwe chinatipanga ife chomwe ife tiri, momwe ife tiriri, kapena ife tikanakhala nawo m—mutu ngati mbalame, kapena chinachake monga choncho; ngati pakanati pasakhale malingaliro a bwana kumbuyo kwa ife kuti apangitse aliyense wa ife akhale ndi mawonekedwe, kuti apange mtengo wa mgwalangwa, mtengo wa thundu, mtengo wa zikunda, n—ndi kusiyantsa pakati pa iyo zomwe i—iyo ili. Kutipanga ife osati ndi . . . ena ali ndi ubweya, ndi ena ndi nthenga, ndi ena ndi zikopa, kuti inu . . . Mwaona, n—ndi malingaliro abwana kumbuyo kwakeko, y—yomwe imalamulira izo. Pakutidi Iye akugwirizira zinthu zonse mu dzanja Lake. Ndipo ine ndikudziwa Iye akhoza kuchita zinthu zonse. Ndipo ife tipempherera izo, ife tipemphera.

347 [Bambo wina akuyankhula kuchokera mwa osonkhana—Mkonzi.] Kukhoza. Ife tiri . . .

348 [Mlongo Snyder akuti, “M’bale Billy, mundikhululukire ine”—Mkonzi.] Inde, mayi, ziri bwino, pitirirani. [Mlongo Snyder akuyankhula “anachiritsidwa” pamene M’bale Branham

anamupempherera iye Lamlungu lina—Mkonzi.] Ameni. Inu mukudziwa, ine ndimayesera kuti ndiganize, Mlongo Snyder, nthawi ina pamene ine ndinali nditaima pano mu kudzoza kuja, ine ndinaganiza. . . Ine ndinamuuzza M'bale Cox, ine ndinati, “Ine sinditi nkomwe kuti ndiyesere za misonkhano yozindikira za mumtima iyo ku Kachisi uko.” O, inu simukudziwa momwe Mdierekezi uyo amandilumira ine, mlongo. Mo—momwe iye amachitira izo! Inu mukudziwa, kumandiuza ine za kuzindikira za mumtima izi.

³⁴⁹ Ndipo kuno, ndinadzapeza kuti alongo awo a Akazi a Wood kuno. . . Ine ndinali ndisanawonepo aliyense wa anthu awo. Gulu la iwo anachiritsidwa pa nthawi imeneyo, ndipo aliyense. . . Bwanji, inu mukudziwa, ndi gawo lalikulu la anthu awo omwe anachiritsidwa. Ndipo zitatha. . . Chinthu chachirendo tsopano; mlongo wawo, ine ndinali nditadya chakudya chamadzulo ndi iye usiku wina, pafupi masabata awiri zisanachitike izo, . . . O, ndi ulendo wonse kupita mpaka mmapiri ku Kentucky, ndipo i—ine ndikungodziwa kuti iye anali ndi liwu longwa la Bambo Wood, ndipo umo simunali mowala kwambiri mchipindamo. Ndipo ine sindinapereke tcheru chirichonse kwa iye mulimonse, ine ndinali, kuyankhula mochuluka kwa mwamuna wake, iye anali atakonzaka kale chakudya. Ndipo ife tinapita panja ndipo tinakakhala pansu ndi kumadya; ndi kubwereranso umo, ine ndinayankhula kwa mwamuna wake, anawukapo ndipo anatuluka panja. Ndipo Mulungu yemwe ali Woweruza wanga mwaulemu akudziwa (nditaima pa guwa ili) ine sindinali kumuzindikira mkazi ameneyo.

³⁵⁰ Ndiyeno utatha msonkhano wa machiritso, ine ndinapanga kuitanira paguwa kwa ochimwa kuti adzalape. Ndipo iye anali wamwano kwambiri motsutsana ndi Izo; ndipo iye analapa napereka moyo wake kwa Khristu, anakweza mmwamba dzanja lake kuti iye akanapereka moyo wake kwa Khristu, ndipo anali akulira. Kudzoza kwina konse kutapita kale; ndikupanga kuitanira kwanga kwa paguwa, ndi zina zotero. Ndiyeno ndinapezeka kuti ndinatembenuka, ndipo apa panali masomphenya, ndipo ine ndinamuwona m'bale wake; yemwe anali mlongo, uyu anali mlongo wake, ndipo iwo ali palimodzi.

³⁵¹ Ndipo ine ndinkaganiza kuti iye anali mkazi wa Charlie, chifukwa ine ndinadziwa nditakhala pa tebulo tsiku lina, kumusi uko k—ku nyumba ya Charlie. . . Mkazi wake wamng'ono, kanthu kakang'ono kwambiri, Ambuye anandisonyeza ine vuto lomwe iye anali nalo. Ndipo kuyambira pa ora ilo lomwe, Ambuye analikhudza thupi lake, atakhala pa tebulo lake apo tsopano. Tony, komwe ife tinali, kumusi uko, tinapita kukasaka agologolo kuja. Ndipo Ambuye analikhudza thupi lake ndipo anatenga chinthu ichi chomwe iye ankayenera kuti azichivala mu wonse wa. . . kwa moyo wake wonse, nkuchichotsa kwa iye; atangokhala apo. Ndipo mkazi

wamng'onoyo nthawizonse ankadyera patali ku mapeto ena a tebuloyo, koma lero, iye anabwera mozungulira kumene, ndipo iye anasunthira mpando wake mkati, ndi amadya pambali pa ine. Iye sanali kudziwa konse chomwe iye anali kuchita. Mwamuna wake atakhala monga *chonchi*, ndi M'bale Bank atakhala apo, ndipo ife tikuyankhula. Ndipo iye anasuntha mozungulira, ndipo iye anakatenga mpando wake, ndipo anadzakhala apa cha pambali panga. Ndipo izo zinali kwa cholinga, Ambuye anawonetsa masomphenya apo pomwe. Ndipo ine ndinamuitana mwamuna wake, chifukwa ilo linali vuto laukazi, ine ndinayamba kumuuzza iye pa zomwe zinachitika. Iye anati, "M'bale Branham, umo ndi ndendende momwe izo zinachitikira, monga choncho." Ndipo apo iye anamuuzza iye, ndipo Ambuye anamuchiza iye. Chabwino.

³⁵² Ndiyeno pamene msonkhano unali utatha usiku wina, ndipo mlongo wina uyu, ine ndinamuwona Charles wamng'ono uyu ndi mkazi uyu palimodzi. Ine ndinaganiza, "Uyo ayenera kuti ndi mkazi wake; koma mkazi wake ndi wa bulondi, ndipo uyu ndi mkazi wa mutu wakuda. Ndipo ine ndinapezeka kuti ndinazindikira masomphenyawo akusunthira ku ngodya cha kuno. Ndipo iye anali atakhala apo akupukuta maso ake ndipo Ambuye anawonetsa masomphenya pambuyo pake iye ata... kuitanira paguwa... utatha msonkhano wa pemphero, kuchiritsidwa kwa odwala, ndipo kuitanira paguwa kunali kutachitidwa, ndipo Mulungu anadikirira mpaka iye atalapa ndipo atapereka moyo wake kwa Iye ndiyeno anatembenuka apo namuchiza iye. Ndipo iye anali nao... mavuto ake anali iye atatupa kwa zaka. Ndipo iye anaphwa mochuluka kwambiri, ndi chirichonse, mpaka ngakhale mapazi ake anachita makwinya pomwe zonse zinali zitachoka pa iye (ziphe) kuchokera ku thupi lake. Akumverera bwino kuposa momwe iye anayamba wamvererapo mu zaka, mwaona. Ndi momwe Ambuye mwa chisomo Chake chodabwitsa amachitira izo! Ine ndikuganiza izo mmomwe ziriri nkhaniyo; sichoncho, Mlongo Wood? Ndi momwe Iye amachitira! M... Mukuti chiani? [Mlongo Wood akuti, "Iye anataya mapaundi seveni sabata yatha"—Mkonzi.] Mapaundi seveni mu sabata. O, Iye ndi Mulungu! Sichoncho Iye?

³⁵³ Tsopano, ine ndikukuuzani inu, chifukwa chomwe ine ndinanenera kwa M'bale Neville... Ine ndimaganiza mwinamwake iye anali ndi uthenga wa usikuuno. Iye anati, "Ayi," iye analibe. Ndipo ine ndiri ndi mafunso angapo pano omwe anatsalira, ine ndinamverera mwachikhalidwe wokakamizidwa kuti ndifike kuno ndi kudzawayankha mafunso awa. Ndiye ine ndiri nawo awiri kapena atatu ena ine mwinamwake sindiwatenga usikuuno.

³⁵⁴ Ine ndikufuna kuti ndikusonyezeni inu ena omwe angoperekedwa kumene kuchokera kwa mlaliki. M'bale Neville basi... kapena Beeler anangwabweretsa iwo kwa ine. [M'bale

Branham akuyankha mafunso eyiti otsatira awa mu Gawo III, kuyambira pa ndime 668, ngati funso nambala 67 kudutsa 74—Mkonzi.]:

Kodi miyalayo ikuimira chiani mu Chivumbulutso 21:19 ndi 20?

Tafotokozani zamoyo zinai za Chivumbulutso 5. . . .Iye akutanthauza 6; si Chivumbulutso 5, ndi 6, ine ndikuganiza.

Ndipo kodi akulu twente-foro ndi ndani?

Kodi chingwe chofiira cha Genesis 38 chinkatanthauza chiani?

Kodi mphatso zizidzatumizidwa kuti zokhudzana ndi imfa ya mboni ziwiri, Chivumbulutso 11?

Kodi oyera adzakhala kuti utatha ulamuliro wa zaka chikwi? Ndipo kodi iwo adzakhala ndi thupi lotani?

Kodi ife tizidzawaweruza chotani angelo?

Ndi tsitsi liti lomwe limakhala la angelo a pa I Akorinto?

³⁵⁵ Mukayankhula za ena abwino, awo ndi ena abwino. Ine mwinamwake sindifika kwa iwo usikuuno, koma ngati Ambuye alola, ine ndidzayesa kuwatenga iwo nthawi ina yomwe ife tidzadzere izo.

³⁵⁶ Ine ndiri nawo ena abwino ndithu ali pano usikuuno; chotero ife tingopemphera tsopano ndi kuwafunsa Ambuye kuti atithandize ife, ndipo ife tilowa molunjika kumene mwa iwo kwa otsatirawa, o, maminiti sate-faifi, forte.

³⁵⁷ Tsopano, Atate Akumwamba odala, ndife oyamikira kwa Inu chifukwa cha zonse zomwe Inu mwatichitira ife. Ndipo, o, ndi zodabwitsa kwambiri momwe chisomo chanu chikufikira kwa ife. Ine ndikuganiza tsopano, usiku wina, ndi mzanga wamng'ono uja wa ine, o, atadwala kwambiri, ndipo Inu munabwera powonekera. Malungo ake anayamba kusweka kuyambira pa ora ilo lomwe, ndipo wathana nawo kwathunthu tsopano. Ine ndikukuthokozani Inu. Ndipo. . . tikungopemphera kuti Inu mukhala ndi wina aliyense yemwe wapempha chopempha usikuuno. Ndipo timadziwa mochepa, mpaka izo zikafika ku nyumba yathu yomwe, chomwe iwo amatanthauza, pemphero laling'ono. O Mulungu, chomwe. . . mo—momwe Inu mumakhalira weniweni. Mu ora ilo pamene dokotala ati adzachokepapo, nkuti, “Ine sindikudziwa, ine sindinayambe ndawonapo chirichonse chikuchita monga choncho,” ndiyeno Ambuye Yesu nkusunthira powonekera.

³⁵⁸ O Mulungu, Ndinu weniweni kwambiri kwa ife, ndipo ndife okondwa kwambiri chifukwa cha izo. Ife tikupemphera kuti Inu mutikhululukire ife pa njira zathu zonse zofooka, ndi njira zathu zopusa. Ndipo, o, muzingotikumbukira ife, Ambuye, kuti ndife mnofu waumunthu mu dziko la mdima, dziko la mdima ndi tchimo ndi chisokonezeko. Ndipo ife tikuyang'ana

kupyolera mu chophimba, momwe ziriri, chiri pa nkhope yathu, ndipo ife tikungowona ndi kudziwa monga timachitira mwa munthu kuno. Koma tsiku lina pamene chophimba icho chidzachotsedwapo, ife tizidzakuwonani Inu maso ndi maso ndi kudziwa monga ife tikudziwidwira. Ndilo tsiku lomwe ife tikuliyembekezera.

³⁵⁹ Ife tikupemphera Atate, tsopano, kuti Inu mutithandize ife pamene ife tikuyesera kuti tipereke kwa anthu Mawu a Mulungu, molingana ndi zopempha zawo. Chotsani matenda onse kwa ife. Ife tikukusowani Inu, Ambuye. Ndipo ife tikupemphera kuti Inu mupereka izo. Lolani zifundo Zanu ziperekedwe kwa ife, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amenii.

³⁶⁰ Tsopano, pa kuyankha mafunso, ine sindiri wopambana mu dzikoli, inu mukudziwa. Koma ine ndikungoyankha mopambana mwa kudziwa kwanga.

³⁶¹ Pano pali limodzi lomwe ine ndinayamba nalo usiku wina, ndipo ine ndinayenera kulekeza:

60. “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu thupi la Khristu.” (Inu nonse mukukumbukira kuti ilo linali funso lomwe ine ndinalipo. Tsopano ilo likupezeka, ndithudi, mu I Akorinto 12) . . . **Pa nthawi yomwe ife tiri . . . kulandira kubadwa kwatsopano, izi zimachitika. Kodi izi . . . Kodi uwu ndi Ubatizo wa Mzimu Woyera, kapena kodi ulipo ubatizo wa mtsogolo, kapena kodi uko ndi kudzazitsako?**

³⁶² Tsopano, apo pali funso ndithu, ndipo ife tikhoza kukhala nthawi yathu yonse basi pa limenelo, ndi usikuuno ndi mawa usiku ndi zina zotero. Izo zingakute . . . izo zinga—izo zingatenge ndi kulimangiriza Baibulo lonse palimodzi. Lemba lililonse liyenera kumamangirizana bwino bwino limodzi ndi Lemba lina lililonse mu Baibulo.

³⁶³ Koma pongoyesera kuzipanga izo mwachidule, momveka momwe ine ndikudziwira kuzipangira kwake izo, ayi; pamene inu mukhulupirira pa Ambuye Yesu Khristu, inu apo mumakhala ndi kubadwa kwatsopano. Pamene inu mukhulupirira pa Ambuye, inu mumalandira lingaliro latsopano, moyo watsopano, koma izo si Ubatizo wa Mzimu Woyera. Mwaona? Inu mumalandira kubadwa kwatsopano pamene inu mukhulupirira, inu mumalandira Moyo Wamuyaya. Iyo ndi mphatso ya Mulungu yomwe inaperekedwa kwa inu kupyolera mu chisomo chayekha pa kuvomereza mphatso yomwe Mulungu akuipereka kwa inu. Mwaona, “Iye amene amva Mawu Anga nakhulupirira pa iye yemwe anandituma ine, ali nawo Moyo Wamuyaya.” Ali nawo moyo wosatha; uko ndiko kubadwa kwatsopano, inu mwatembenuzidwa, izo zikutanthauza kuti inu “mwatembenukira kwina.”

364 Koma Ubatizo wa Mzimu Woyera umakuikani inu mu thupi la Khristu, kuti mulandire mphatso za utumiki. Iwo sumakupangani inu kukhala Mkhristu mochulukirapo, iwo umangokuikani inu mu thupi la mphatso. Mwaona? “Tsopano, mwa Mzimu umodzi” (1 Akorinto 12) “ife tonse timabatizidwa kulowa mu thupi limodzi. Tsopano,” akutero Paulo, “pali mphatso zosiyana, ndipo mu thupi ili muli mphatso zisanu ndi zinai.” Ndipo mu thupi ili... Inu mumayenera kuti mubatizidwire kulowa mu thupilo kuti mukhale nayo imodzi ya mphatso izi. Izo zimabwera limodzi ndi thupilo.

365 Koma, tsopano, tikanena za kukhala nao Moyo Wamuyaya ndi kukhala Mkhristu, iwe umakhala Mkhristu mphindi imene iwe umakhulupirira. Tsopano, uko sikudzipangitsa kukhulupirira, uko ndi kukhulupirira moona pa Ambuye Yesu ndi kumulandira Iye ngati Mpulumutsi wako wako; iwe umabadwa katsopano apo pomwe, ndipo umakhala nao Moyo Wamuyaya. Mulungu amabwera mkati mwa iwe.

366 Tsopano penyani, Moyo Wamuyaya; Yesu anati, “Iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya, ndipo sadzabwera mu chiweruzo koma wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo.” Ndiwe choredgedwa chatsopano apo pomwe. Ndiye Paulo anakomana nawo ena a anthu awo, uko mu Machitidwe 19. Iwo anali naye mlaliki uko komwe yemwe anali wazalamulo wotembenuka dzina lake Apollo. Ndipo Apollo anali mwamuna wamphamvu mu Malemba, ndipo iye anali kutsimikizira mwa Malemba kuti Yesu anali Khristu. Mwaona?

367 Tsopano penyani. Apollo, kupyolera mu Mawu, anali akutsimikizira mwa Mawu. “Chikhulupiro chimadza pakumva, kuwamva Mawu. Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine, ali nawo moyo wosatha.” Mwamvetsa izo? Apollo, mwa Mawu, anali akutsimikizira. Ndipo awa anali Akhristu, iwo anali otsatira, ophunzira. Ndipo Apollo anali kutsimikizira mwa Mawu, kuti Yesu anali Khristu. Ndipo iwo anali ndi chisangalalo chachikulu ndipo anawalandira Mawu, komabe akudziwa ubatizo wa Yohane wokha.

368 Ndipo pamene Paulo anadutsa kuntunda kwa magombe a Efeso, iye anakawapeza ophunzira awa ndipo iye anati, “Kodi inu munalandira Mzimu Woyera *kuchokera* pamene inu munakhulupirira?” Mwaona?

369 Tsopano, pamene inu mukhulupirira, Yesu anati, “Inu mumakhala nao Moyo Wamuyaya.” Uko ndiko kubadwa kwatsopano. Uko ndi kutembenuka kwanu, kusinthika. Koma Ubatizo wa Mzimu Woyera ndi mphamvu ya Mulungu kuti inu mwabatizidwiramo ndipo ndinu oyenera kulandira mphatso zisanu ndi zinai zauzimu izi kuti zizigwira ntchito kupyolera mwa inu; monga ngati, kulalikirira, alaliki, atumwi, abusa,

aneneri, . . . ndi mphatso zonse za thupilo zimafika mkati umu, pamene inu mwabatizidwa kulowa mu thupi ili. Ndipo izo . . . sizimakupangani inu kukhala Mkristu mochulukira konse, izo zimangokukhazikitsani inu mwapamalo pa malo oti mukhale mzimu wotumikira mu Mpingo wa Mulungu wamoyo. Tsopano mwazimvetsa izo? Mwaona?

³⁷⁰ Tsopano funso ndilo . . . Tiyeni tingowayankha iwo limodzi ndi limodzi, pali mafunso atatu.

“Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu thupi la Khristu.”

Uko ndi kulondola, 1 Akorinto 12 angapereke yankho kwa izo. Chabwino.

Pa nthawi iyo yomwe ife timalandira kubadwa kwatsopano, izi zimachitika? Kodi izo ndi pamene?

³⁷¹ Ndi chimene iwo akufuna kuti achidziwe, inde . . . “Mwa Mzimu umodzi . . .” Ayi. Ayi. “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu thupi limodzi.” Mwaona, apo si pamene kubadwa kwatsopano kumayambira, kubadwa kwatsopano kumayambika pamene iwe *ukhulupirira* pa Ambuye Yesu.

³⁷² Tsopano onani, palibe . . . palibe chinthu chimodzi . . . Tsopano mvetserani. Kodi inu mungachite chiyani kupatula kukhulupirira? Ndi chiani chinanso chomwe inu mungathe kuchita? Inu mungachite chiani pa izo moonjezeranso kuposa kungokhulupirira izo? Ndiuzeni ine chinthu chimodzi chimene inu mungakhoze kuchichita. Palibe chinthu chimodzi chimene inu mungathe kuchita kunja kwa kukhulupirira Iwo. Tsopano, ngati chirichonse chingabwere kunja kwa kukhulupirira kwanu, icho si kuchita kwa inueni, ndi kuchita kwa Mulungu. Chotero . . .

³⁷³ Tsopano ngati ife tinganene kuti pamene inu . . . Nthawi zambiri ine ndawonapo, nthawi zambiri, anthu akulandira “umboni woyambirira wa kuyankhula mu malirime” ngati Mzimu Woyera. Ndipo nthawizina amawagwedeza anthuwo, kapena kuwamenya iwo ndi kuwasisita iwo, nkumati, “Yankhulani iwo. Yankhulani iwo. Yankhulani iwo. Yankhulani iwo.” Inu mukudziwa, zibwereza bwerezani mawu, “Yankhulani iwo. Yankhulani iwo. Yankhulani iwo.” Mwaona, ndi chinachake chimene inu mukuchipanga enianu. N—n—ndipo izo sizi . . . izo sizima . . . i—izo si kanthu. Inu mukhoza kupeza chisokonezeko cha malirime. Inu mukhoza kupeza z—zinthu zochuluka, ndi zomverera. Koma ngati chirichonse chibwera kunja kwa chikhulupiriro chanu chanu chomwe, iyo iyenera kukhala mphatso Yaumulungu ya Mulungu itaperekedwa kwa inu. Mwaona?

³⁷⁴ “Ndipo mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu thupi limodzi.” Uko nkulondola, mwaona. Ubatizo

wa Mzimu Woyera ndi kachitidwe kosiyanana ndi kubadwa kwatsopano. Kwina ndi kubadwa, kwina ndi ubatizo. Kumodzi kumakubweretserani inu Moyo Wamuyaya, kwina kumakupatsani inu mphamvu. Iko kumapereka mphamvu yolowa mu Moyo Wamuyaya, mwaona, kuti izigwira ntchito. Tsopano mwazimvetsetsa izo? Chabwino. Chabwino.

³⁷⁵ Tsopano pano pali lina, likubwerapo kachiwiri, opambana omwe ine ndinali nawo usiku uja:

61. Kodi unali kuti mzimu wa Yesu masiku atatu omwe thupi Lake linali mmanda? Mzimu Wake unali kuti?

³⁷⁶ Tsopano, mzimu Wake, ngati inu mungawatsatire Malemba, . . . chabwino, ife tikhoza kungobweretsa malo ambiri. Koma, ine ndikudabwa, n’ndani ali ndi Baibulo? M’bale Stricker, inu muli nalo Baibulo? Chabwino. M’bale Neville, inu muli nalo lina? Ndipezereni ine Masalmo 16:10. Ndipo n’ndani wina? Mlongo Wood, inu muli nalo Baibulo apo? Chabwino, M’bale Stricker, (chabwino, aliyenseyo), inu mundipezere ine Machitidwe 2:27, Machitidwe 2:27.

³⁷⁷ Ndipo tsopano, malo oyamba, pamene Yesu anafa, . . . Pamene inu mufa, thupi lanu limafa. Mawu oti *imfa* amatanthauza “kulekanitsa,” kulekanitsidwa basi ndi okonedwa anu. Koma apa Iye ananena izi, mu Yohane Woyera, mutu wa 11, “Iye amene amva . . .” Osati . . . Ine ndikupempha kukhulukira kwanu; izo ziri mu Yohane Woyera 5:24, “Iye amene amva Mawu Anga ali nawo Moyo Wamuyaya.”

³⁷⁸ Yesu anati kwa Marita, yemwe anabwera kuti adzakomane ndi, . . . Iye anati, “Ngati Inu mukakhala muli kuno, m’bale wanga sakanati afe. Koma ngakhale tsopano, chirichonse chimene Inu muti mumupemphe Mulungu, Mulungu apereka icho kwa Inu.”

³⁷⁹ Iye anati, “Ine ndine chiukitsiro ndi Moyo.” Mwaona? “Iye amene akhulupirira mwa Ine, ngakhale iye atafa, komabe iye adzakhalana moyo; ndipo aliyense yemwe akhala moyo nakhulupirira mwa Ine, sadzafa konse.”

³⁸⁰ Tsopano—tsopano, pali gawo la ife limene silimafa. Ndipo monga ine ndabwera kumene kudutsa mu mzere wa Malemba, chirichonse chomwe chiri ndi chiyambi chiri ndi mapeto. Ndi zinthu zomwe ziribe chiyambi, zomwe ziribe mapeto. Chotero pamene ife timulandira Khristu, Mulungu, ife timakhala ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, ndipo Moyo wathu umangokhala wopanda malire monga Moyo wa Mulungu uli wopanda malire; ife tiri nawo Wamuyaya.

³⁸¹ Tsopano, mawu oti *kwanthawizonse*, ife takhala tikudutsa mu izo. Mawu oti *nthawizonse* ndi “danga la nthawi,” kwanthawi *ndi* (cholumikizira) kwanthawi. Ndipo ife tinapezapo apa kuti izo ziri—izo ziri ndi mathero, basi monga

kuvutika konse, ndi matenda onse, ndi zodandaulitsa zonse, ndi chilango chonse, ndi gehena iyoyomwe ili ndi mathero.

382 Koma Moyo Wamuyaya ulibe mathero, chifukwa Iwo unalibe chiyambi. Iwo sungakhoze konse kufa chifukwa Iwo sunabadwe konse. Iwo unalibe chiyambi cha masiku, Iwo ulibe mathero a nthawi. Tsopano, njira yokha yomwe ife tingakhalire moyo Mwamuyaya, ndi kupyolera mu kulandira chinachake chomwe chiri Chamuyaya. Ndipo Mulungu anali; pasanakhale chirichonse, kunali Mulungu. Mulungu analibe konse chiyambi kapena mathero.

383 Ndipo Mulungu anali Mzimu waukulu uwu. Ife tinamujambula Iye ngati—mitundu seveni ya utawaleza yomwe imaphimba. . . Uta womwe kwenikweni umaphimba dziko lonse ngati iwo ukanati usamaligunde dziko lapansi. Amangokhala ali madzi mu nkombero wa kupindika kwa dziko lapansi, kumene kumapangitsa izo. Koma, tsopano, monga Mulungu ali Wamuyaya, ndipo Iye anali Wangwiro: chikondi changwiro, mtendere wangwiro, chisangalalo changwiro, kukhutitsidwa kwangwiro. Mizimu yonse isanu ndi iwiri iyo (pamene ife tizifika mu Chivumbulutso), iyo inatuluka umo; zinadzapanga Mulungu, zinali ungwiro. China chirichonse kunjira kwa izo chakhala chiri chinachake chomwe chinali chitapotozedwa kuchokera kwa Izo.

384 Tsopano njira yokha yomwe ife tingakhoze kubwerera ku ungwiro, ndi kubwerera limodzi ndi Ichho (ungwiro, womwe uli Mulungu). Ndiye ife tibwera ku ungwiro, ndiye ife tiri nawo Moyo Wamuyaya; wopanda mathero, kapena wopanda—wopanda chirichonse, kungokhala kwanthawizonse Moyo Wamuyaya.

385 Tsopano iye akuyankhula za solo. . . mzimu. Pakuti ife timanyamula matupi athu kupita ku manda a oyeretsetsa a ife, a thupi ili. Ndipo thupi. . . Mu malo oyamba, pamene Mulungu, Logos yomwe inachokera kwa Mulungu. . .

386 Kapena, monga ine ndinadutsa mu izo, Akatolika amachitcha Ichho, “umwana Wamuyaya wa Mulungu.” Chimene, monga ine ndinanena kale, mawuwo samapanga ngakhale chanzeru. Mwaona, sikungakhoze kukhala kuli mwana Wamuyaya, chifukwa mwana anayenera kukhala ndi chiyambi. Ndipo chotero Yesu anali ndi chiyambi, Mulungu analibe chiyambi. Mwaona? Koma Mwana anali. . . osati umwana Wamuyaya, koma Mwana yemwe anali ndi Atate pachiyambi anali Logos yomwe inatuluka kuchokera kwa Mulungu.

387 Ndipo iyo inali fiofane ya Mulungu imene inatuluka. Mawonekedwe a umunthu omwe analibe maso monga inu mumapenyera; diso labwinoko. Iyo inalibe makutu monga inu mumamvera, koma kumva kwambiri kwa patali. Mwaona, Iyo inali fiofane, yomwe, utawaleza wonse uwu unadzichepetsramo mu—f—fiofane. Mose anawona Iyo pamene Iyo inkadutsa pa

thanthwe monga choncho. Iye anawona gawo la ku nsana, anati, “Iye ankawoneka ngati munthu.”

³⁸⁸ Abrahamu anamuwona Iye pamene Iye anadzalowa mu mnofu wa umunthu ndi kudya mwana wang’ombe, nkumwa mkaka wina, kudya batala. Abrahamu anamuwona Iye pamene Iye anangolowa umo, ndiyeno anasowa pomwepo kwa izo. Ife tikupeza kuti matupi athu ndi opangidwa ndi zipangizo sikisitini za dziko lapansi, izo zimangobwera palimodzi. Ndipo Mulungu anaziika izo palimodzi, ndipo anawaika Angelo awiri mu matupi amenewa; Angelo omwe ankaima ndi kumayankhula. Ndipo Angelo anali anthu nthawi ina . . . ndi pa nthawi iyo.

³⁸⁹ Tsopano zindikirani, ife tikupezano kuti, Melkizedeki anali ndani koma Mulungu Mwiniwake! Uyo sakanakhoza kukhala wina aliyense, pakuti Iye anali Mfumu ya Salemu yomwe ili Yerusalemu. Iye anali wopanda bambo ngakhale amayi; sakanakhoza kukhala Yesu, chifukwa Iye anali nawo abambo ndi amake. Iye analibe chiyambi cha masiku, analibe mathero a moyo; alipo Mmodzi yekha yemwe ali nazo izo, ameneyo ndi Mulungu. Uyo anali Mulungu akukhala kuno mu fiofane. Mwaona? Zindikirani, Mfumu ya Salemu.

³⁹⁰ Tsopano, Mulungu wakhala moyo kupyola mu m’badwo, kupyolera mwa anthu Ake. Anali Mulungu yemwe anali mwa Davide, yemwe anamupangitsa iye kukhala pa phiri, ndi ngati mfumu yokanidwa, ndi kulira. Mzimu uwo womwe unawonetseredwa mwa Yesu Mwana wa Davide, yemwe anakandwa mu Yerusalemu ndipo analira.

³⁹¹ Yosefe, anagulitsidwa zidutswa zitatu za ndalama, ankadanidwa ndi abale ake, anakondedwa ndi abambo ake, anakhazikitsidwa ku dzanja lamanja la Farao, ndipo palibe munthu akanakhoza kubwera kupatula mu . . . kubwera kudzera kwa Yosefe, ndipo lipenga linkalira ndipo bondo lirilonse linkagwadira kwa Yosefe: choimira mwangwiro cha Khristu. Uwo unali Mzimu wa Khristu ukukhala moyo kupyolera mwa amuna awo. Mwaona?

³⁹² Tsopano, tsopano apa pamene Yesu anafa, anali Mulungu atawonetseredwa mu thupi. Mulungu anadzakhala munthu. Mu malamulo a chiwombolo, njira yokha yomwe munthu akanakhoza kuwombolera chuma chotaika cha Israeli, iye ankeyenera kukhala ali wa pachibale. Iye ankeyenera kuti akhale wapachibale wapafupi. Bukhu la Rute limafotokoza mokongola izo; ndipo iye ankeyenera kuti akhale wapachibale. Koteri Mulungu ankeyenera kuti akhale wapachibale kwa munthu, polinga kuti munthu akhoze kukhala wapachibale kwa Mulungu. Mwaona?

³⁹³ Iye ali nawo mzimu mwa iye, munthu ameneyo pamene iye amabadwa, chifukwa iwo ndi mzimu wa chibadwa. Iwo ndi

mzimu wa mdziko, iwo ndi mzimu wa—mulungu wa mdziko muno. Iye ndi mphukira chabe ya Adamu.

³⁹⁴ Mtengo umadzibala wokha. Zomera zimadzibala zokha. Zinyama zimadzibala zokha. Anthu amadzibala okha. Iwo ndi zopangidwa kuchokera ku chirengedwe cha pachiyambi. Mukuzimvetsa izi?

³⁹⁵ Tsopano, tsopano pamene munthu abadwa, iye amabadwa ndi mzimu mwa iye wa mdziko muno. Ndicho chifukwa iye amayenera kuti abadwe kachiwiri. Pakuti mzimu uwu unabwera kuchokera pa kukhala ndi pakati kwa bambo ndi mayi, komwe kunali kukhala ndi pakati kwa kugonana, ndipo mwamtheradi sakanakhoza kumakhala moyo kwanthawizonse. Kotero iye amayenera kuti abadwe kachiwiri. Ndipo iye asanazichite izo, Mulungu anachita kutsika pansi ndi kudzakonza njira yoti iye azibadwa kachiwiri; chifukwa iye analibe njira yoti adziwombolere yekha, iye anali wopanda chiyembekezo. Iye analibe... anali wopanda chiyembekezo, wopanda Mulungu, wopanda Khristu, mu dziko, atataika ndipo atapita. I— iye... panalibe kanthu komwe iye akanakhoza kuchita kuti adzipulumutse yekha. Iye... c hirichonse... Ziribe kanthu ngati iye akanakhala wansembe wamkulu, kaya iye akanakhala bishopu, kaya iye akanakhala papa, chirichonse chomwe iye akanakhala, iye akanakhala basi ndi wolakwa monga munthu winayo.

³⁹⁶ Chotero, izo zinachita kutengera Wina yemwe sanali wolakwa, kuti achite izo. Ndipo Mmodzi yekha yemwe anali wosalakwa anali Mulungu Mwiniwake. Ndipo Mulungu anachita kutsika pansi ndi kudzakhala munthu (ndipo Iye anabwera mu mawonekedwe a Khristu) kuti akazike mbola ya imfa, kuti achotsepo mbola ya imfa, kuti atiwobole ife, kuti ife... osati mwa ntchito zathu kapena mwa ubwino wathu (ife tiribe uliwonse), koma mwa chisomo Chake, kuti tipulumutsidwe. Ndiye ife timalandira za Moyo Wake zinalowa mu thupi lachivundi ili, ndipo tsopano ndife ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, ndipo tiri nawo Moyo Wamuyaya mkati mwathu. Iye ndi ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Chotero, Yesu, pokhala wamoyo... .

³⁹⁷ Ndipo palibe munthu, ziribe kanthu momwe aliri woipa kapena momwe aliri wabwino, pamene iye ayenera... pamene iye amachoka pa dziko lapansi ili, iye si wakufa. Iye ali kwina kwakenso. Koma iye ali nawo moyo womwe uti udzawonongeke, iyeyo atatha kulangidwa mu gehena chifukwa cha zochita zake, iye... komabe moyo uwo uyenera kuti uthe. Pali mtundu umodzi wokha wa Moyo Wamuyaya.

³⁹⁸ Tsopano, ife takhala tikudutsa mu izo. Ngati munthu angakhale wochimwa ndi kudzalangidwa kwanthawizonse... Iye sangakhoze kulangidwa kwanthawizonse kupatula ngati iye ali ndi Moyo Wamuyaya. Ngati iye ali ndi Moyo Wamuyaya,

iyе ndi wopulumutsidwa. Mwaona? Kotero pali mtundu umodzi wokha wa Moyo Wamuyaya, ndipo uwo ndi Zoe, “Moyo wa Mulungu.” Ndipo iye sangakhoze kuwonongeka.

³⁹⁹ Koma oipa ali mu malo o—odikirira (mozunzidwa) ku chiweruzo chawo (kuti adzaweruzidwe molingana ndi ntchito anazichita mu thupi) pa tsiku lotsiriza. Tsopano, koma ife . . . Machimo a anthu ena amapita patsogolo pa iwo, ena amawatsira pambuyo iwo.

⁴⁰⁰ Tsopano ngati ife tivomereza machimo athu, Iye ndi wokhulupirika kuti atikhulukire ife, chotero ife sitidzasowa konse kuti tidzaimе pa chiweruzo cha Mulungu. Inu mukuzimvetsa izo? Penyani, Aroma 8:1, “Chotero palibe tsopano kutsutsika kwa iwo omwe ali mwa Khristu Yesu.” Omwe ali MWA Khristu. Omwe adutsa kuchokera ku imfa napita ku Moyo; mwaona, ife tiribe kutsutsika amene tiri mwa Khristu Yesu. “Omwe sitimayenda momvera thupi, koma momvera Mzimu.” Mwaona? “Iye amene amvera Mawu Anga, nakhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya.”

⁴⁰¹ Ndipo ngati ine ndavomerezedwa mwa Khristu, ndipo Khristu anatenga chiweruzo changa, ndipo ine ndinavomereza chitetezero Chake kwa machimo anga, Mulungu angakhoze bwanji kundiweruza ine? Iye anandiweruza kale ine, pamene Iye anamuweruza Khristu. Ndiye ndine mfulu kwa chiweruzo. “Ndiye pamene ine ndiwona magazi, Ine ndidzadutsa pa inu.” Mwaona?

⁴⁰² Koma, tsopano, woipa sali chomwecho. Iye amapita ku malo a kuzunzidwa. Ndipo ife tikudziwa kuti izo nzoona. Woipa ali moyo. Iye ali mu malo a kuzunzidwa. Iye ali mu malo momwe iye sakuwadziwa . . . Umo ndi momwe azamizimu awa ndi asing’anga amayitana mizimu iyi ya anthu omwe anapita kale, mtundu wina wa zosewera ndi nthabwala zauve ndi zinthu zomwe iwo amazinena, ngati inu munayamba mwawonapo zirizonse za izo. Chabwino. Bwanji? Iwo sama . . .

⁴⁰³ Tayang’anani pa Abiti Pepper ууу, nkhani yanga isanapite ya *Chozizwitsa cha Donny Morton*. Ndi angati anayiwerenga nkhani imeneyo? Inde, ambiri a inu munatero, zedi. Ndipo iyo ili mu *Reader’s Digest*. Kodi inu munazindikira, basi izo zisanapite Abiti Pepper, wazamizimu wamkulukulu yemwe dziko linayamba lamudziwapo. Masamba thwelofu anaperekedwa kwa nkhani yake. Ndipo kwa zaka fifite . . . Iwo akhalapo naye iye mu dziko lonse, ndi kutsimikizira kwasayansi ndi chirichonse, kuti “iye mwamtheradi amayankhula ndi okufa, ndipo anthu amabwera uko.” Nchiani? Dzina la Mulungu silinatchulidwe konse nthawi imodzi, palibe kulapa, palibe machiritso Auzimu, palibe kanthu kena ka Izo, mwaona.

⁴⁰⁴ Chinthu chokha chomwe chinali, chinali anthu awo akutchulidwa, “John, kodi iwe sukundidziwa ine? Ine ndi

George yemwe anali ku malo *akuti akuti*, ndipo ine ndinachita *zakuti-n-zakuti* ndi *zakuti-n-zakuti*. Kodi iwe ukuwakumbukira malo aja omwe ife tinapitako kumusi kuja ndi kukachita izi?" Mwaona, ndi zonse zomwe iwo amazidziwa. Iwo apita. Adutsa kuchokera...Iwo a—iwo palibe kanthu kawatsalira koma chiweruzo.

⁴⁰⁵ Komwe mtengo umatsamira, ndi komwe iwo umagwera. Ndipo momwe inu mumafera...Nchifukwa chake ine ndimasiyana ndi zowapempherera okufa, mwaona, mapemphero oyimira pakati k—kapena kuyankhulana ndi oyera ndi zina zotero. Izo sizingakhoze kukhala ziri, malingana ndi Mawu a Mulungu. Izo ziribe ubwino uliwonse kumupempherera wina aliyense iye atapita kale. Iwo atha. Iwo...iwo...Iwo adutsa mzere wa pakati pa chifundo ndi chiweruzo. Iwo mwina apita ku chifundo, kapena apita kutali ndi chifundo. Yesu ananena chomwecho, mu mutu wa 16 wa Mateyu Woyera, I—I—Iye anaphunzitsa izo; mutu wa 16 wa Marko, ine ndikukhulupirira apo pali. Bambo wolemera ndi Lazaro; palibe munthu angakhoze kuliwoloka phompho ili, ndipo sadzaliwoloka konse! Ndi inu apo. Mwaona? Kotero izo zikukhazikitsa icho.

⁴⁰⁶ Tsopano, koma pamene Khristu anafa, chirichonse chinkayenera kuti chichitire umboni kuti Iye anali Khristuyo. Tsopano tiyeni tipite ku funso lanu. Chinthu choyamba, nyenyezi zinakana kuti ziwale, dzuwa linalowa, mwezi sunapereke kuwala kwake, dziko linasanza miyala yake, pa imfa Yake. Ndipo Iye anapita ndipo anakalalikira kwa miyoyo yomwe inali mu ndende, yomwe siinalape mu kupirira kolalika kwa mu masiku a Nowa. Iye, iwo ankayenera kuti azindikire. Tayang'anani pa izo! Ndipo ngati mwa mwayi pangakhale pali wochimwa pano usikuuno, ganizira izo miniti. Tsiku lina Uthenga uwu umene inu mukuumba ukulalikidwa pakali pano, inu mudzayenera mudzachitire umboni ndi Iwo. Kwinakwake inu mudzagwada bondu lanu, mosasamala yemwe inu muli. Izo zikhoza kukhala zaka teni sauzande kuchokera lero, izo zikhoza kusakhala mpaka...mmawa. Lirilonse lomwe liti lidzakhale, inu mudzagwada penapake, ndipo inu mudzaumba Uthenga uwu womwe ukulalikidwa mobwereza kwa inu nomwe.

⁴⁰⁷ Pakuti miyoyo iyo itakhala kale mu ndende, yomwe siinalape pamene Enoki ndi pamene onse awo anakalalikira, ndi Nowa... ndi pa kupirira motalika kwa Mulungu, monga izo ziriri tsopano, poyembekezera kuti nthawi iyo ifike. Ndipo Nowa ndi Enoki ndi onse awo analalikira, ndipo anthu awo ankaseka ndi kumawanyogodola iwo. Ndipo iwo anali mu nyumba ya ndende, ndipo Yesu anapita ndipo anakalalikira kwa miyoyo yomwe inali mu ndende. Iye anachitira umboni! Miyamba inachitira umboni, "Iye anali!" Dziko lapansi linachitira umboni, "Iye anali!" Gehena anachitira umboni, "Iye anali!"

408 Baibulo linanena kuti izo... Davide, zaka zambiri kalelo, mu Masalmo... Chabwino, M'bale, inu werengani Masalmo, ngati inu mungatero apo. Masalmo 16:10: [M'bale Neville akuwerenga, "Pakuti inu simudzawusiya moyo wanga mu hade; ngakhale kulola Woyera wanu Uyo kuti awone chivundi."—Mkonzi.]

409 Werengani chinthu chomwecho, m'bale, pamene Petro ankalalikira; pa Machitidwe, mutu wa 2, ndime ya 27: [M'bale Stricker akuwerenga, "Chifukwa inu simudzawusiya moyo wanga mu hade, ngakhale kuti inu mudzalola Woyera wanu Uyo kuti awone chivundi."—Mkonzi.]

410 Werengani ndime ziwiri pamwamba pa iyo, m'bale, chotero kuti inu mukhoze kuimvetsa nkhaniyo—nkhani yakeyo: [M'bale Stricker akuwerenga, "Pakuti Davide akuyankhula zokhudza Iye, ine ndinawawoneratu Ambuye—Ambuye nthawizonse patsogolo pa nkhope yanga, pakuti iye ali ku dzanja langa lamanja, kuti ine ndisasunthidwe. Chotero mtima wanga ukusangalala, ndipo lirime langa likukondwera; kuwonjezera apo mnofu wanga nawonso udzapuma mu chiyembekezo. Chifukwa inu simudzaisiya solo yanga mu hade, ngakhale inu simudzalola Woyera wanu Uyo kuti awone chivundi."—Mkonzi.]

411 Werengani ndime yotsatirayo tsopano: [M'bale Stricker akuwerenga, "Inu mwandidziwitsa ine njira za moyo; inu mudzandipanga ine wodzaza ndi chisangalalo ndi nkhope yanu."—Mkonzi.]

412 Inde, zindikirani. Tsopano, mzanga wa Mboni za Yehova, ine ndikufuna kuti ndikufunsi inu za izo. Mwaona? Ngati hade ali malo... Hade, Sheol, chirichonse chimene inu mukufuna kuwatcha iwo; ngati izo zimathera kumanda, ndiye nchifukwa chiani Iye anati, "Ine sadzaisiya solo Yanga mu hade, ngakhale inu simudzalola kuti awone chivundi?" Nanga bwanji izo? Mwaona?

413 Apa thupi Lake linali, mu manda; ndipo solo yake inali mu hade, akulalikira, wamoyo! Nanga bwanji zimenezo? Iye anali mu fiofane Yake kachiwiri. Solo yake inali kumusi uko ndi anthu awo omwe anali mu fiofane nawonso. Ndipo anali akuchitira umboni kwa iwo, omwe "sanalape mu kupirira kotalika."

414 Iye... Mwa kuyankhula kwina, Iye anagogoda pakhomo. Ndipo pamene chitseko chinakankhika nkutseguka, ndipo kwa miyoyo yonse yomwe siinalape, Iye anati, "Ine ndine Mbewu ya mkazi. Ndine Iye yemwe Enoki kuno... ." Uko mu Paradiso, malo ena. Musati konse muwataye malo atatu awo, tsopano: malo a oipa, malo a olungama, ndi hade iyoyeni. Mwaona?

415 Monga ngati utatu wa Kumwamba, ngati: Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Ngati utatu wa chirombo: mneneri wabodza, chirombo, n—ndi chilemba cha chirombo. Ndi zonse

izo, kumbukirani, zonsezo ziri mu utatu. Utatu umapanga chimodzi, kupangidwa changwiwo. Chimodzi chimakhalitsidwa changwiwo. Inu mumakhala wangwiwo, chimodzi mwa zitatu: solo, thupi, ndi mzimu; madzi, magazi, ndi misempha. Mwaona, chirichonse chomwe inu muli, inu muyenera kuti kutenga zitatu kuti zipange chimodzi changwiwo. Mutenge chidutswa cha galasi cha ngodya zitatu ndipo muike dzuwa pa icho, inu mukhala ndi utawaleza wangwiwo. Mwaona, chirichonse, inu mumayenera kukhala ndi zitatu kuti mupange chimodzi changwiwo.

416 Ndipo tsopano, kumbukirani izo, pamene Iye anafa, Iye anapita choyamba nakalikirira kwa miyoyo yomwe sinali mu ndende. . . yomwe inali mu ndende, ndipo anakachitira umboni kuti Iye anali “Mbewu ya mkazi.” Iye anali “Mmodzi yemwe Enoki anamuwona akubwera ndi zikwi khumi za oyera Ake.” Iye anali woti achitire umboni Malemba omwe anali atalalikidwa ndi Nowa, ndi Enoki, ndi wolungama, kuti “Iye anali Mmodzi uyo.” Chirichonse chinkayenera kuti chichizindikire Icho!

417 Ndiye Iye anatsikira mu hade, ndipo anakalandira mafungulo a imfa ndi hade kuchokera kwa Mdierekezi.

418 Anabwereranso mumtunda mpaka mu Paradiso; ndipo anakawatengako Abrahamu, Isaki, ndi Yakobo, ndi wolungama; ndipo anawutsa (Mateyu 27), ndipo iwo anatuluka kuchokera mmanda nakalowa mu mzinda, ndipo anawonekera kwa anthu akuyenda mu msewu. Aleluya! Ndi inu apo!

419 Tsopano, koma thupi lake. . . Pamene solo Yake inali cha kuno ikuchitira umboni kwa otaika, pansi apa ukutenga mafungulo kuchokera kwa Mdierekezi, ndi kubwererako nkumubweretsa Abrahamu ndi Isaki; solo Yake inali itagona mu. . . solo Yake inali pansi uko ikuchita izo, ndipo thupi Lake linali litagona mmanda. Ndi chifukwa Yesu anati. . . Anthu akuti, “Chabwino, bwanji Yesu amati, ‘Masiku atatu, Ine ndidzaliutsa ilo. Masiku atatu Ine ndidzaliutsa ilo.’? I—Iye anafa Lachisanu madzulo, anauka Lamlungu mmawa.”

420 Koma penyani, izo zinali “*mkati mwa masiku atatu*,” ngati inu mutapeza lexicon. Pakuti Iye ankadziwa kuti Davide, pansi pa kudzoza (kudzoza kwa Mzimu Woyera), anati, “Ine sindidzalola Woyera wanga Uyo kuti adzawone chivundi.” Iye ankadziwa kuti izo zinkanena za Iye. Iye ankadziwa izo zinkatanthauza Iye. Iye anali Woyera Uyo wa Mulungu, ndipo Iye ankadziwa kuti chivundi chimalowamo mu maora seventethuu. Kwinakwake mkati mwa masiku atatu awo, Iye anali woti atuluka kuchokera umo kachiwiri, chifukwa Malemba sangakhoze kusweka.

421 Ndipo lonjezo lirilonse mkati Umo limanena za ine ndi kunena za inu, ndi zathu!

422 Iye anati, “Inu liwonongeni thupi ili, ndipo ine ndilidzutsa ilo mu masiku atatu.” Pakuti Iye anati, “Ine sindidzaisiya solo

Yanga mu hade, ngakhalenso sindidzalola Woyera Wanga Uyo kuti awone chivundi.”

423 Iye ankadziwa, mu masiku atatu thupi ilo likanati lituluke kuchokera umo. Iye sanakhalemo masiku atatu athunthu. Ayi, bwana, Iye ndithudi sanatero. Iye anangokhala kuchokera Lachisanu madzulo mpaka Lamlungu mmawa, palibe khungu limodzi la thupi ilo likanakhoza kuvunditsidwa.

424 Ndipo Iye anali atafa, ndipo anakonzedwa, ndipo anali atagona...kapena atakulungidwa mu nsalu, ndipo atagonekedwa mmanda. Mu dziko lotentha, lalowe, kungotenga maora pang’ono ndipo Iye ayamba kuvunda. Inu muyamba ku...kuwonongeka, inu mukudziwa, thupi lake, mphuno yake kugwera mkati ndi zinthu, chivundi kuyambika umo; dziko lotentha ilo, lachinyezi. Ndipo ilo likanayamba kuvunda, chifukwa ilo linali thupi. Koma Iye ankadziwa, khungu ilo lisanavunde, kuti Mulungu ananena kupyolera mwa Davide mneneri, “Ine sindidzalola Woyera Wanga Uyo kuti awone chivundi.”

425 Momwe Iye anawatengera Mawu a Mulungu ndi kukhala moyo ndi Iwo! Tsopano, limodzi lililonse la malonjezo awo mkati umo omwe ankanena za Iye, Mulungu analikwaniritsa lililonse la iwo. Ndipo lonjezo lililonse lomwe limanena za wokhulupirira, Mulungu adzalikwaniritsa lonjezo lililonse la Iwo. Amen. Mungokhala otsimikiza kuti Izo ndi Choonadi. Amen. Chotero, moyo Wake... .

Kodi inu mukuganiza izo ziri... .Ayi, ine ndikupepesa. Kodi mzimu wa Yesu unali kuti mu masiku atatu pamene thupi Lake linali mmanda?

426 Mzimu Wake unali mu hade, pansu mu zigawo zotsikirapo; ndipo Iye anauka. Ndipo ine ndikhoza kuwonjezera kakang’ono—nenso laling’ono apa lomwe lingakhoze kukuthandizani inu mmagawo onse. Pamene Iye anauka, Lake...Pamene Iye anauka kuchokera kwa akufa, Iye mwamtheradi anali asanathane nayo ntchito ya chiwombolo apobe. Uko nkulondola. Iye an kayenera kuti achitsuke chinthu chonsecho kwathunthu. Mtengo unali utalipidwa, koma kuwopsya kuja kwa hade, kuwopsya kuja kwa manda... .Ndipo apa, pamene i—pamene Iye anafa, Iye anapita patsogolo choncho. Iye sanasiye kugwira ntchito pamene Iye anafa, Iye anapitiriza kulalikir!...?. .Ndikhululukireni pa kachitidwe kanga kosakhala bwino, ine ndikulingalira, koma Iye sanasiyize konse!

427 Inu simudzafa konse! Thupi thupi likhoza kupuma kwa kanthawi, koma Mulungu adzaliutsa ilo apo, Iye analonjeza kuti Iye akanadzatero. Koma inu simungawonongekenso monga Mulungu sangakhoze kuwonongeka. Ndiko kulondola. Penyani, Lake...Iye atafa kale, kwa chiani...atafa kwa ophunzira.

Iye anali akugona, chomwe Iye anali. Iwo anamugonetsa Iye; momwe Iye ananenera za Lazaro, “Ine ndikupita ndikamuutse iye.” Mulungu anachita kumuutisa Iye.

⁴²⁸ Penyani, Iye anapitabe mpaka pansi, Iye anapitiriza kulalikira. Ndipo Iye anakalalikira kwa miyoyo kuno mu ndende. Anapitabe mpaka ku hade, anakatenga mafungulo kuchokera kwa Mdierekezi. Anabwereranso pamwamba ndipo anakalalikiranso mu paradiso, ndipo anauka nabwereranso pamwamba pa tsiku lachitatu. Anakacheza ndi ophunzira Ake kwa masiku makumi anai, ndipo pa kutha kwa tsiku la makumi anai, Iye anapita mpaka mmwamba; chifukwa, chirichonse pamwamba pa ife, zamatsenga ndi china chirichonse... Iye anadula matsenga aliwonse, kukaikira kulikonse, ndipo anapanga mzere wa pemphero kuchokera pa dziko lapansi mpaka ku Ulemerero pa kukwera Kwake. Anakwera mmwamba ndipo anakakhala pansi pa dzanja lamanja la Ufumu Wake. Mgonjetsi! Mgonjetsi Wamkulu, mwamtheradi. Imfa sikanakhoza kumugwira Iye! Hade sikanakhoza kumugwira Iye! Dziko lapansi silikanakhoza kumugwira Iye!

⁴²⁹ Pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, Iye anapatsidwa... Iye anapita ku mzinda wotsikitsitsa ndi kwa anthu otsikitsitsa, ndipo anapatsidwa dzina lotsikitsitsa. Ndi chimene munthu anachita kwa Iye. Iye anapita ku Yeriko, mzinda wotsikitsitsa. Munthu wochepetsetsa anachita kukwera pamwamba mu mtengo kuti ayang’ane pansi pa Iye. Ndi pamene munthu anamuika Iye. Iye anali wosambitsa mapazi, ntchito yoipisitsa yomwe ikanakhoza kuperekedwa. Iye anadzakhala wotsikitsitsa. Ndipo Iye ankatchedwa dzina lotsikitsitsa lomwe likanakhoza kuperekedwa, *Bezebule*, “kalonga wa adierekezi.” Munthu anamupatsa Iye dzina lotsikitsitsa, malo otsikitsitsa, ndipo anamutumiza Iye ku zigawo zotsikitsitsa za gehena wotsikitsitsa.

⁴³⁰ Mulungu anamuukitsa Iye umo ndipo anamutumiza Iye ku Miyamba Yammwambamwamba, ndi Dzina loposa dzina lililonse. Aleluya! Bwanji, Iye azichita kumayang’ana pansi, kuti awone Kumwamba. Mpando wanu wachifumu wakwezedwa pamwamba pa miyamba ya Kumwamba. Ndi Dzina lalikulukulu lomwe linayamba latchulidwapo Kumwamba ndi pa dziko lapansi linayenera kuti... ndipo linamangiridwa momuzungulira Iye. Ndi chimene Mulungu anachita kwa Iye. Munthu anamuika Iye potsikitsitsa, ndipo Mulungu anamupanga Iye Wammwambamwamba. Apo Iye anali, kuchokera kotsikitsitsa kukhala Wammwambamwamba.

⁴³¹ Iye anakhala chotsikitsitsa kuti Iye akhoze kutibweretsa ife pamwamba Kummwambamwamba. Iye anakhala ife, kuti ife kupyolera mu chisomo Chake tikhoze kukhala Iye, ana aamuna a Mulungu. Ndiko kumene Iye anapita. Ameni! Lidalitsike Dzina Lake. Iye anapanga njira yomwe ife tingakhoze kupitako,

nafenso, tsiku lina, “Chifukwa Ine ndiri moyo, inu mukhala moyo nanunso.”

⁴³² O, palibe zodabwitsa... Pamene munthu awagwira masomphenya amenewo, sipanayambe pakhala munthu akanakhoza kuzifotokoza izo. Iwo ayesera ngakhale kuti azifotokoze izo, nasokonezeka malingaliro awo; nyimbo yaikulu iyi: “*O chikondi cha Mulungu, kulemera kwake ndi ungwiro; Kusafotokozeka kwake ndi mphamvu.*” Ndime yotsiriza ija... kapena ine ndikukhulupirira ndime yoyamba, iyo ili: “*Ngati ife ndi inki yodzaza nyanja, ndipo mlengalenga mutapangidwa chipepala;...*” Inu mukudziwa kemene iyo inapezedwa? Italembedwa pa amisala... pakhoma la ku malo aamisala. Palibe munthu angakhoze konse kuchifotokoza Chikondi cha Mulungu icho. O, icho sichingakhoze kunenedwa, chomwe Iye anatichitira ife. Mai, inu mungakhoze bwanji kuika phindu limodzi kunjira kwake? Ndi chisomo Chake, kuchokera pa chiyambi mpaka ku mapeto. Ine ndinataika, wothedwa, ndi wopanda chondithandiza, wopanda pabwino, wopanda kanthu nazo, ndipo Iye mwa chisomo Chake anabwera ndipo anadzatipulumutsa ife. O, mai. Ndicho Chake... Awo ndiwo Ambuye anga. Ndicho chikondi Chake, uwo ndi ubwino Wake.

⁴³³ Tsopano ife tatsala ndi pafupi maminiti seveni ndi pafupi mafunso fikitini.

62. Kodi inu mukuganiza kuti ndi koyenera kuti akazi azigwira ntchito yawoyawo kunjira kwa mpingo?

⁴³⁴ Inde. Ilo langokhala funso, basi... osati funso la mwamalemba, koma... Ndithudi, ine ndikutero. Inde, bwana, ndife tonse antchito palimodzi. Akazi ali nawo malo awo, ndipo ndithudi iwo ali nawo. Inde, bwana. Zingogwirani ntchito yanu yanu yomwe inu mungakhoze kuichita, ndipo Mulungu azikudalitsani inu chifukwa cha iyo.

Chabwino, tsopano tiyeni tiwone:

63. Chonde tafotokozani utatu. Kodi Mwana angakhoze bwanji kukhala pa dzanja lamanja la Atate, akutetezera... kwa Atate, ngati iwo si anthu awiri?

⁴³⁵ Chabwino, mzanga wokonedwa, ndizo... i—ilo ndi vumbulutso. Ngati Yesu anati, “Ine ndi Atate Anga ndife mmodzi,” ndiye iwo angakhoze bwanji kukhala awiri? Mukuona? Tsopano, iwo si awiri.

⁴³⁶ Mkazi nthawi yina ananenapo kwa ine, ndipo ine ndinali kufotokoza izo, anati, “Inu ndi akazi anu—ndinu awiri, komabe ndinu mmodzi.”

⁴³⁷ Ine ndinati, “Koma, Mulungu ndi Mwana ziri mosiyana ndi izo, mwaona.” Ine ndinati, “Inu mukundiwona ine?”

“Inde.”

“Inu mukuwona akazi anga?”

“Ayi.”

438 Ine ndinati, “Ndiye, Atate ndi Mwana ndi zosiyana; Yesu anati, ‘Pamene inu mukundiwona Ine, inu mukuwaona Atate.’” Mukuona?

439 Atate ndi Mwana. . . Atate anali Yahova Wamphamvuzonse (Mulungu) akukhala mu kachisi wotchedwa Yesu Khristu, yemwe anali Mwana wa Mulungu wodzozedwa. Yesu anali munthu, Mulungu ndi Mzimu. Ndipo palibe munthu anamuwonapo Mulungu pa nthawi iliyonse, koma wobalidwa yekha ndi Atate wamuonetsera Iye. Iye anali. . . Iye. . . umunthu Wake, thunthu Lake. Umulungu Wake, chirichonse chomwe Iye anali, Iye anali Mulungu! Iye sanali china chocheperapo kapena china choonjezera kuposa Mulungu. Komabe, Iye anali munthu. Iye anali munthu, nyumba yomwe Mulungu anali kukhalamo. Ndiko kulondola, Iye anali malo okhalamo Mulungu.

440 Tsopano, ngati inu mukufuna Malemba ena pa izo. . . M’bale Neville, ngati inu mungandipezere ine Marko Woyera 14:62. Ndipo Mlongo Wood, inu mundipezere ine Aefeso 1:20. Winawake ali ndi Baibulo? Chabwino, kwezani mmwamba dzanja lanu. Mlongo Arnold, inu muli nalo lina kumbuyo uko? Chabwino, inu ndipezereni ine Machitidwe 7:55. Chabwino. Marko 14:62, M’bale Neville; ndi Mlongo Wood ndi Aefeso 1:20; Machitidwe 7:55, Mlongo Arnold.

441 Chabwino, inu muli napo apo, M’bale Neville? Chabwino, werengani tsopano: [M’bale Neville akuwereanga, “Ndipo Yesu anati, Ine ndine: ndipo inu mudzamuwona Mwana wa munthu atakhala padzanja lamanja la mphamvu, ndipo akubwera mmitambo ya kumwamba.”—Mkonzi.]

442 Chabwino, tsopano, penyani manenedwe oyambawo apo. Yesu anati, “INE NDINE.”

443 “INE NDINE.” Ndi ndani anali INE NDINE? Sipanayambe pakhala munthu mu dziko lonse akanakhoza kuzitanthauzira Izo. Ngakhale. . . inu amene mumawerenga lexicon ndi zina zotero, sipanayambe pakhala munthu yemwe akanakhoza kutchula. . . Ndi J-v-h-u. Ndipo ngakhale masikolala Achihebri sakanakhoza kulitchula Ilo. Chisamba choyaka hijia kuja, tsiku lija pamene Iye anakomana naye Mose, Uyo anali J-v-h-u. Chotero iwo ankalitchula Ilo “J-o-h, Yehova,” koma Izo si “Yehova.” J-v-h-u, mukuona, palibe yemwe akudziwa.

444 Ndipo inu mukuti, “Chabwino, Mose sankakhoza kulitchula Ilo.”

445 Iye anati, “Ine ndingakati ndani?”

446 Iye anati, “Ukati, ‘INE NDINE’ wakituma iwe. INE NDINE.”

447 Tsopano penyani. *INE NDINE* ndi tensi ya pakali pano, osati “Ine ndinali” kapena “Ine ndidzakhala ndiri,” INE NDINE.

Tsopano, Iye anati, “Ichi chidzakhala chikumbutso podutsa mu timibadwo tonse: INE NDINE.”

448 Tsopano tayang’anani pa Yesu ataima apa pa phwando tsiku lijali. Iwo anati, “Ife tikudziwa tsopano iwe ndi wamisala.” Mawu olondola, “Iwe ndi wamisala” (*misala* ndi “kupenga”). “Ife tikudziwa kuti ndiwe wopenga. Ndiwe Msamaria, iwe uli ndi chiwanda.” (Yohane Woyera, mutu wa 6) Ndipo iye anati, “Tsopano, iwe ukuti ndiwe. . . unamuwona Abrahamu, ndipo iwe ndi bambo wa usinkhu wa zaka zosapitirira fifite?” (Iye mwina ankawoneka wokulirapo pang’ono kwa usinkhu Wake, koma Iye anali sate zokha, koma ntchito Zake). . . Anati, “Iwe ukutanthauza kuti iwe uli bambo wosapitirira usinkhu wa zaka fifite, ndipo ukuti iwe ‘unamuwona Abrahamu’? Ife tikudziwa iwe ndi wopenga tsopano.” Mwaona?

Iye anati, “Asanakhalepo Abrahamu, INE NDINE.”

449 “INE NDINE,” Iye anali INE NDINE wamkuluyo. Apa Iye akuwauza Ayuda awa kachiwiri, mwaona, “INE NDINE! Ndipo pamene inu mudzandiwona Ine ndikubwera pa dzanja lamanja la mphamvu. . .” Ndi kulondola uko?

450 Werengani izo kachiwiri, m’bale: [M’bale Neville akuwerenga, “Pamene inu mudzamuwona Mwana wa munthu atakhala pa dzanja lamanja la mphamvu, ndipo akudza mmitambo ya kumwamba.”—Mkonzi.]

451 Werengani lanu tsopano, Mlongo Wood: [Mlongo Wood akuti, Aefeso 1:20?—Mkonzi.] Inde, mayi. [Mlongo Wood akuwerenga, “Zomwe iye anachita mwa Khristu, pamene iye anamuukitsa iye kwa akufa, ndipo anamukhazika iye pa dzanja lake lomwe lamanja mu malo ammwambamwamba.”—Mkonzi.]

452 Chabwino, werengani lanu, mlongo. Mwaona, Ndi chimodzimodzi basi: [Mlongo Arnold akuwerenga, “Koma iye, pokhala wodzaza ndi Mzimu Woyera, anawoneka mokhazikika kumwamba, ndipo anawuwona ulemerero wa Mulungu, ndi Yesu ataima pa dzanja lamanja la Mulungu.”—Mkonzi.]

453 Tsopano, inu mukuona, Mulungu sakanakhala ndi dzanja lamanja lalikulu, mwaona, ndi Yesu ataima pa dzanja Lake lamanja. *Dzanja lamanja* limatanthauza “ulamuliro.” Mukuona? Basi mwachitsanzo, bwanji n—ngati ine ndikanakhala ndi kulumulira kwakukulu kwa mpingo, kapena ine ndikanakhala bishopu wa mtundu wina, ndipo M’bale Neville nkutenga malo anga, iye akanakhala munthu wakudzanja langa lamanja. Mwaona, izo zikutanthauza kuti iye. . . iye akanakhala wa ku dzanja lamanja langa.

454 Tsopano, Yesu ali ku dzanja lanu lamanja la Mphamvu. Tsopano, Iye akunena chomwecho, apa mu Aefeso, pamene iye akufotokoza izi, Iye ali pa dzanja lamanja la mphamvu. “Mphamvu zonse Kumwamba ndi padziko lapansi” (Iye anatero, chitachitika chiukitsiro Chake) “zapatsidwa mmanja Mwangwa.

Ine ndiri nazo mphamvu zonse Kumwamba ndi pa dziko lapansi. Pitani inu chotero ndi kukaphunzitsa mafuko onse, nkuwabatiza iwo mu Dzina la Atate, ndi Mwana, Mzimu Woyera, kuwaphunzitsa iwo kuti azisunga zinthu zonse zomwe Ine ndakulamulirani inu; taonani, Ine ndiri ndi inu nthawizonse, mpaka ku mathero a dziko.”

455 “Mphamvu zonse Kumwamba ndi pa dziko lapansi.” Ndi kuti uko. . . Ngati kuli mulungu uko pambali pa Iye, iye ndi wopanda mphamvu. Mwaona, sikungakhoze kukhala kuli Mulungu wina. “Mphamvu zonse za Kumwamba ndi pa dziko lapansi” ziri mdzanja Lake. Chotero, inu mukuona, “Iye waima pa dzanja lamanja,” (momwe munthuyu anafunsira funsoli), sizikutanthauza. . .

456 Tsopano onani! Thupi. . . Mulungu ndi Mzimu. Eya, ndi angati akumvetsa izo? nenani “Ameni.” Mulungu ndi Mzimu, Yesu ndi Munthu, ndipo Yesu anali Mulungu atapangidwa thupi. Yesu anali. . . Ife sitingakhoze konse kumuwona Mulungu, mwaona, Iye ndi Mzimu. Inu simungakhoze kuwona mzimu. “Palibe munthu anayamba wamuwonapo Mulungu pa nthawi iliyonse.” Palibe munthu akanakhoza kumuwona Mulungu.

457 Ndipo ndiloleni ine ndinene izi, “Inu simunayambe mwandiwonapo ine.” Inu simunayambe mwandiwonapo ine mu moyo wanga wonse, ndipo inu simudzandiwona konse ine. Ndiko kulondola. Inu mumaliwona thupi ili lomwe limafotokoza za munthu uyu yemwe ali mkati umu. Tsopano, thupi ili liribe Moyo Wamuyaya, koma mzimuwo uli nawo Moyo Wamuyaya. Thupi ili lidzabwerera kwao, koma ilo lidzatulukiranso kachiwiri mu mawonekedwe ake basi, monga njere ya tirigu imapita mu nthaka. Chikhristu chakhazikika pa chiukitsiro, osati kusinthanitsa. Chiukitsiro; Yesu yemweyo anapita pansi, Yesu yemweyo anabwereranso. Ngati inu mudzapita pansi muli wa mutu wofiira, inu mudzabwererako muli wa mutu-wofiira; ngati inu mupita pansi muli wa mutu wakuda, inu mudzatulukira muli wa mutu-wakuda. Mwaona, ndi chiukitsiro.

458 Pamene inu muti muzidya. . . Ine ndinamufunsa izo dokotala, si kale litali, ine ndinati, “Bwanji kuti pamene ine ndinali wa usinkhu wa zaka sikisitini. . . Nthawi iliyonse pamene ine ndimadya, ine ndimaonjezera moyo wanga?”

459 Ndinati, “Uko nkulondola.”

460 Inu mumalowetsamo zatsopano—makhungu atsopano nthawi iliyonse inu mumapanga. . . m—mnofu kumapanga. . . kapena chakudya chimapanga makhungu a magazi, ndipo khungu la magazi ilo limakupangani inu kukhala wamphamvuko. Ndi momwe inu mumakhallira moyo. Ndiye, chinachake chimayenera kuti chife nthawi iliyonse, kuti iwe ukhale moyo. Tsiku lirilonse, chinachake chimafa: ngati inu mudyanya nyama, ng’ombe inafa; kapena chirichonse chimene inu

mumadya; ndipo nsomba inafa; k—kapena tirigu anafa, kuti apange mkate; mbatata inafa, yomwe inapanga mbatata; ndi . . . mawonekedwe aliwonse a moyo; inu mukhoza kukhala moyo kokha kupyolera mu zinthu zakufa.

⁴⁶¹ Ndipo inu mukhoza kukhala moyo Mwamuyaya kokha chifukwa chinachake chinafa: Yesu. Osati chifukwa inu munajowina mpingo, osati chifukwa inu munabatizidwa, osati chifukwa munavomereza Chikhristu; chifukwa inu munavomereza Moyo wa Yesu Khristu umene unakhetsedwa . . . magari omwe anakhetsedwera kwa inu, ndipo inu munamulandira Iye ngati Mpulumutsi wanu wanu.

⁴⁶² Tsopano, zindikirani, ine ndifunse izi. Ine ndikufuna kuti ndikufunse *inu* izi. Tayang'anani pa ichi, ndi chokongola. Mwinamwake ine ndinaphunzitsapo izo kale (ine sindikudziwa) kuno; ukamalalikira konsekonse, iwe umaiwala zomwe unanena kwina . . . kumalo ena. Koma, nchifukwa chiani izo ziri, ndiye . . .

⁴⁶³ Tsopano, ine ndikulingalira, Mlongo Smith . . . ine sindikudziwa ngati ine ndimamudziwa M'bale Fleeman kumbuyo kutali uko kapena ayi. Ndi Tryphena, ine ndikumukumbukira iye pamene iye anali mtsikana wamng'ono. Inu mukundikumbukira ine, pamene ine ndinali ndiri . . . ndinali bambo wamng'ono, wamfupi, wojinja; wa tsitsi lakuda, la mzindo. Ine ndinkamenya nkhonya. O, ine ndinkaganiza kuti ine ndinali munthu wamasewero kwambiri mu dziko. "O," ine ndinkaganiza, "kunalibe wina aliyense akanadzakhoza kundimenya ine. Ayi, bwana." Koma i—ine ndinakhala woposisidwa ndi izo, inu mukuona. Koma i . . . Tsopano, ine ndinkangoganiza, "O, mai." Ine ndinkaganiza, "Ngati inu mukanakhoza kuika chinthu ichi pa nsana pangala, ine ndikanayenda mu msewu ndi icho." Zedi, panalibe chinkandivuta ine. Ndipo nthawi iliyonse yomwe ine ndinkadya, ine ndinali ndikukulirapo ndi wamphamvupo nthawi zonse. Nthawi iliyonse yomwe ine ndinkalowetsamo moyo watsopano . . . Ine ndinkadya kabichi, mbatata, ndi nyemba, ndi nyama, basi monga ine ndikuchitira lero. Ndipo ine ndinkakhala wamphamvupo ndi wamkulupo nthawizonse. Ndipo pamene ine ndinafika poti ndinali pafupi twente-faifi . . .

⁴⁶⁴ Ine ndikudya mwabwinoko tsopano kuposa momwe ine ndinkachitira apo, inu nonse omwe mukundidziwa ine, mukudziwa zimenezo. Ine ndikhoza kudya mwabwinoko tsopano, tonse a ife tiri. Koma nchifukwa chiani izo ziri, M'bale Eagen, ndiye, ngati ine ndikadali kudya chakudya chabwinoko, chochuluka cha icho, mavitamini abwinoko ndi chirichonse . . . Ndipo pamene ine ndikudya mochulukira, ine ndikufota pang'ono pang'ono. Ndipo tsopano ine ndikukhala bambo wokalamba wa mapewa okugwa, wa mutu wa dazi, ndi kukhala wa imvi, ndi manja akuchita makwinya, nkhope

ikugwera mkati, mapewa akupita pansu, mmawa zimandivuta kuti ndidzuke, ndi. . . O, mai. Nchifukwa chiani izo ziri choncho? Ngati ine ndikuonjezera moyo wanga nthawi iliyonse yomwe ine ndikudya, nchifukwa chiani izo ziri ndiye?

⁴⁶⁵ Ngati ine ndiri kutsanulira madzi mu chikho kuchokera mu dende, ndipo ilo nkudzadza mwatheka, ndiyeno nkuyamba kumachepamo nthawi yonseyo mmalo mokwera mmwamba; ndipo ndikamatsanuliramo ochulukira, mofulumira iwo nkumacheperamo. Ndi inu apo. Ndipo inu simungakhoze kutsimikizira izo mwasayansi ngati inu mukanati mutero. Bukhu ili ndi chinthu chokha chomwe chingatsimikizire izo kuti Mulungu anakonzeratu; ndi kukonzeratu, Mulungu anatiwona ife tikubwera.

⁴⁶⁶ Inu bambo achikulire, ndi inu akazi achikulire, mwinamwake ena a amuna anu—ndi akazi anu mwina akhoza kukhala atapita kale. Izo ziribe—izo sizivutitsa chirichonse. Alaluya. Iwo angodutsa chotchinga kwinko, akudikira; mwamtheradi. Ndipo iwo akuyembekeza kuti adzakhale ndi inu kachiwiri. Ndi kulondola, zedi, iwo ali. Iwo akukhumba kudzakhala nanu limodzi kachiwiri. Baibulo linati iwo ali, miyoyo ya pansu pa guwa ikulira, “Ambuye, mpaka liti?” Mwaona? Iwo sali mu chikhalidwe chawo choyenera.

⁴⁶⁷ Mulungu sanatipange konse ife Angelo, iye anatipanga ife amuna ndi akazi. Ife nthawizonse tidzakhala tiri amuna ndi akazi, chifukwa ife tiri—chopangidwa cha luntha la Mulungu lomwe. Ife tikhoza nthawizonse kumakhala amuna ndi akazi.

⁴⁶⁸ Koma ndiyeno nchiani? Mwaona, mwinamwake inu mukuganiza kuti pamene inu munayenda kupita ku guwa, inu ndi wokondedwa, munanena kuti ife tikutengana wina ndi mzake kukhala mkazanga wokwatitsidwa movomerezeka ndipo tizikhala limodzi mu chikhalidwe choyera cha chilumikizano ichi, n—zisomo za Mulungu ndi zina zotero, ndi umboni wanu wonse umene inu munapereka, ndilo lonjezo lanu lomwe inu munalipanga. Chinthu choyamba inu mukudziwa, munayamba kuzindikira, nonse inu. Iye anali woongoka, ndi tsitsi lowala; ndipo mamiyo ali maso ake okongola, aang’ono, abulauni, kapena maso a buluu, kapena chirichonse chomwe iwo anali. O, momwe inu munkayang’anira pa iye. Inu munayenda mukutuluka, munayang’ana pa adadi, “Momwe, mapewawo anali owongoka”; ndipo patapita kanthawi iwo anayamba kugwa. Amayi adzayamba mutu wa imvi, nyamakazi zinayambikamo ndi zina zotero. Ndipo patapita kanthawi, ulendo iye anapita, kapena iye anapita basi.

⁴⁶⁹ Chinali chiani icho? Pamene Mulungu anakuwonani inu mutaima apo, Iye anati, “Ndi zimenezo, umo ndi momwe ine ndikukufunira inu.” Chabwino, imfa, iwe bwerapo, koma iwe sungakhoze kuwatenga iwo mpaka ine nditakuloleza iwe.

470 O, o, ine ndikuganiza za Yobu. Inde, Mulungu anali kuyang'ana pansi, Yobu ankadziwa kuti Mulungu ankamukonda iye. (Ndipo zindikirani iye sangakhoze kukutengani inu.) Iye anati, "Iwe uli naye iye mmanja mwako, koma iwe usautenge moyo wake."

471 Ndiyeno chinthu choyamba inu mukudziwa, mapewa anayamba kugwa, ndipo patapita kanthawi inu munali mutapita. Nchiani chomwe chinachitika?

472 Tsopano, mu chiukitsiro simudzakhala chinthu chimodzi chomwe chizidzayimira imfa. Sikungakhoze kukhala kuli chinthu chimodzi choyimira dziko lapansi lino, cha zomwe... Mwaona, inu munabwera kuno mwa chifuniro cha Mulungu, inu munali ndi moyo. Ndiye imfa inalowamo, nkukutengerani inu pansi. Mukudya chakudya chomwecho ndi chirichonse, mukumwa mtundu womwewo wa madzi, chirichonse; koma imfa inadzalowa umo. Koma chithunzicho chinali chitaikidwa kale. Aleluya. Mu chiukitsiro inu mudzakhala muli moyo kachiwiri. Ndipo padzakhala popandanso imfa, kapena chofanana ndi imfa, kapena ukalamba, kapena kulumala kapena chirichonse. Mwachisavundi, ife tidzaima mofanana Naye, angwiro kwanthawizonse. Aleluya. O, i... Izo zingamupangitse aliyense kufuula, makamaka pamene inu mwafika mu usinkhu wangawu.

473 Usinkhu wanga uli, ine ndikulingalira, npamene inu mumaganizira za izo, kuposa kale. Inu mumangokhala pa mtundu wa kusintha uko, inu mukuona. I... Iwe umayamba kumadabwa, "Nchiani chonse ichi? Kodi ine ndachita chiani?" Ine ndimayang'ana mmbuyo kuno, ine ndimaganiza, "Mai, ubwino wanga; chabwino, kodi iye wapita kuti, Ambuye? Ndine pano, wausinkhu wa zaka forte-eyiti. Zaka zina ziwiri, ine ndikhala theka la zana. Pfyuu. Ine ndiri kokha..."

474 Tangoyang'anani pa miyoyo yochepa yomwe ine ndaipindula. Ine ndimafuna kuti ndipindule mamilioni ndi mamilioni ena. Mulungu, andithandize ine. Ine ndimadzichitira manyazi ndekha ngakhale kuti ndibwere kunyumba pa tchuthi. Kuganiza, "O, zokolola zacha, ndipo antchito ali apang'ono. Mamilioni ali mu tchimo ndi manyazi akufa tsiku lirilonse, mvetsera ku kuitana kwawo." Ine ndimapita kukagona uko usiku ndipo ndimawamva achikunja osauka aang'ono awo akukuwa kutali mu dziko. Momwe iwo amadzera mwa zikwi, akumadzandikoka ine, n—ndipo ataima apo pa bwalo la ndege komwe iwo amakhala ndi ankhondo kumeneko kuti awaike iwo mmbuyo, kuti adzangomva nkhani ya Yesu Khristu.

475 Ndipo kuno ife timachita kupempha, ndi kulengeza mu pepala ndi china chirichonse, ndi kuwapezera iwo malo abwino kwambiri kuti akhalemo, zosangalatsa zabwino kwambiri ndi kuimba kwabwino, iwo amabwera ndiye "Oooo, chabwino, ine

ndikulingalira izo nzabwino, ngakhale si za mchikhulupiriro changa.”

476 O, mai, motani—motani—kodi—k—kodi zingatenge nthawi yaitali bwanji?” Izi si . . . izi zoyenera. Ndipo kuno ife timataira mazana a mabilioni a matani a chakudya motayira zonyansa, ndipo anthu awo akanazilandira izo mokondwera. Ndipo iwo ndi zolengedwa za dziko lapansi mofanana ndi ife. Mai, ife . . . Chabwino, izo sizingakhoze kukhalapo nthawi yaitali choncho.

477 Chabwino, tsopano, Atate ndi ndani? Atate ndi Mwana ali mmodzi. Penyani, mu 1 Yohane 5:7, Ilo linati, “Alipo atatu omwe amachitira umboni Kumwamba, Atate, Mawu (omwe ali Mwana) . . . Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera: atatu awa ali mmodzi.”

478 “Ziripo zitatu zomwe zimachitira umboni pa dziko lapansi, zomwe ziri madzi, magari, ndi Mzimu.” Ndizo zinthu zitatu zomwe zinadza kuchokera mu thupi la Khristu. Iwo anamupyosa mu mbali Yake: madzi anatulukamo, Magazi anatulukamo, “Mmanja Mwanu Ine ndikuwupereka Mzimu Wanga.” Ndi inu apo, ndizo zinthu zitatu. Zitatu izi si chimodzi, koma izo *zimagwirizana* mu chimodzi.

479 Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera; 1 Yohane 5:7, amati, “Atatu awa *ali* Mmodzi.”

480 “Madzi, magari, ndi Mzimu *zimagwirizana* mu chimodzi.” Osati Mmodzi, koma *zimagwirizana* mu chimodzi. Kotero Atate . . . Ndipo chinthu chokha chomwe thupi lingakhoze kuchichita, pamene Mulungu angakhoze kudziwona Yekha, kuti kupyolera muchilango chomwe thupi ili linadutsamo, apo pali kudutsana . . . kudutsana apo pomwe, inu mukuona. Apo ndi pamene Iye amawaona Magazi awo ataima pakati pa Iye ndi chiweruzo. Apa pali Mawu Ake, anati, “Tsiku limene inu mudzadya, tsiku limenelo inu mudzafa.” Ndipo apa Yesu anati, “K . . . Koma ine ndinatenga malo awo. Mwaona, ine ndinatenga malo awo.”

481 Mukuikumbukira nkhani yanga usiku wina pamene ine ndinawona masomphenya a mkazi woyipa kwenikweni yemwe anali mu chipinda uko? Ndipo ine ndinakhala ndikumutsutsa iye, ndinkati, “Mulungu, bwanji inu simukungowaphulitsa malowo?” Ndiye Iye anandisonyeza *ine*, mwaona. Ndipo ine ndinayenda kupita kwa iye ndipo ndinakamuuza iye zomwe zinachitika.

Tsopano, ili ndi funso langa lotsiriza.

64. Kodi inu mukuganiza, malingana ndi malemba, kuti Ayuda adzakhala . . . adzambulandira Khristu basi mkwatulo wa Mpingo usanachitike?

482 I—i—ine ndimakhulupirira kwenikweni kuti mkwatulo wa Mpingo . . . Uku ndi kulingalira kwanga kwanga, mwaona.

Ndipo ngati ife tikadakhala ndi nthawi, ife tikanazitenga izo nkuzidutsitsa, koma iyo—yapitirira pa naini tsopano. Penyani, ine ndikukhulupirira kuti Ayuda adzamulandira Khristu pa kudza Kwake kwachiwiri. Tsopano kumbukurirani, kuti munthuyu adziwe izi, maso athu anachititsidwa khungu...kapena maso awo anachititsidwa khungu kuti ife tikhoze kulandira kupenya kwathu. Aliyense akudziwa, Malemba amayankhula za izo. Kodi uko nkulondola? Paulo amatiuza ife...kuti ife tinachititsidwa khungu...kuti Ayuda anachititsidwa khungu mwa cholinga kuti ife tikhoze kumulandira Khristu. Mwaona? Ndipo ife ndi mpesa wa kuthengo womwe unamezanitsidwa umo pa kuleredwera mu mtengowo.

⁴⁸³ Tsopano lingaliro langa ndi ili, ine ndikupatsani inu... Iwo andifunsa ine, “Kodi inu mukuganiza...?” Tsopano umu ndi momwe ine ndikuganizira kuti zidzachitikira. Ine sindikudziwa. Chirichonse chomwe icho chiri, ine ndikutsimikiza kuti mwa chisomo cha Mulungu ndi chifundo Chake, ife tidzakakhala kumeneko; mwaona, mwa chisomo Chake, chirichonse chomwe icho chiri. Ine mwina sindingathe kuzilingalira izo, koma pano pali zomwe ine ndikuganiza. Ine ndikukhulupirira kuti ife tiri pa nthawi yotsiriza. Ine ndikukhulupirira m’badwo wa Amitundu ukutha pakali pano. Ine ndikukhulupirira ife tiri pa kutsekera.

⁴⁸⁴ Ndipo tsopano Ayuda; pano pakhala pali zinthu ziwiri zomwe zinawachimwa Ayuda: Iwo anachititsidwa khungu, iwo sanakhoze kuziwona izo; ndipo chifukwa chakuti Amitundu, kwa chinthu chimodzi, nthawi zambiri... .

⁴⁸⁵ Ine ndinkayankhula kwa Myuda ku Benton Harbor, Mlongo Smith, ndipo inu mukudziwa zomwe Iye ananena kwa ine? (uko kwa mmodzi wa Aisraeli awo... malo a Israeli uko) Funso ili la kuchiritsidwa kwa munthu wakhungu. Ndipo iye anati, “Inu simungakhoze kuwadula Ayuda m... Inu simungakhoze kumudula Mulungu mu nthuli zitatu ndi kumupereka iye kwa Myuda; kumupanga iye Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.” Anati, “Inu simungakhoze kuchitira izo kwa Myuda, ife si opembedza mafano.” Anati, “Ife timakhulupirira mwa Mulungu *mmodzi*.” Mwaona?

⁴⁸⁶ Ndipo inu mukamamupanga Mulungu atatu: Mulungu Atate, Mulungu Mwana, ndi Mulungu Mzimu Woyera; inu ndithudi mungamuchititse khungu Myuda apo pomwe, chifukwa iye amadziwa bwinoko. Iye amadziwa bwinoko kuposa izo. Izo zingakupangeni inu wopembedza mafano motsimikiza basi monga kupembedza mafano kuli, inu muli ndi amulungu atatu. Inu muyenera kuti muwapange iwo kukhala Mulungu yemwe yemweyo, awo si amulungu atatu, ndi maudingo atatu a Mulungu yemweyo. Mwaona, Mulungu anatumikira mu utate, Iye anatumikira mu umwana, ndipo Iye akutumikira tsopano mu nyengo ya Mzimu Woyera. Mulungu mwini yemweyo.

487 Ndicho chifukwa ife tinalamulidwira kuti tizibatiza mu Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera; chifukwa, osati mu dzina la . . . Mu *Dzina*, osati maina, osati mu maina kapena mu dzina la Atate, mu dzina la Mwana, mu dzina la Mzimu Woyera; koma “mu Dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.” Mwaona, kumuzindikira Mulungu mwini yemweyo kukhala ali Khristu. Mwaona, ndi Yemwe iye ali, izo sizingakhoze kukhala mwanjira inanso. Mwaona? Ndipo Lemba . . .

488 N—ndiyeno ngati vumbulutso lathu liri lolakwika, ndiye Petro ndi atumwi ena onsewo ankaphunzitsa chinthu cholakwika; chifukwa munthu aliyense mu Baibulo ankabatizidwa mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Palibe munthu mmodzi yemwe anayamba wabatizidwapo mwa “Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” ndi chiphunzitso cha Chikatolika. Ine ndikhoza kutsimikizira izo kwa inu mwa mawu awo omwe, ndi lexicon yawo yomwe ndi chirichonse. Ndi Kachikhulupiro ka Chikatolika ndipo osati—ndipo osati chiphunzitso cha Baibulo. Ndipo palibe munthu . . .

489 Ngakhale Mfumu yaku England inabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu. Pafupi zaka sikisi handiredi pambuyo pa imfa ya mtumwi wotsiriza, pamene sikunkatchedwa nkome England, iko kunkatchedwa “Dziko Laangelo.” Ndi komwe ilo linachokera, dzinalo. Iye anabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu.

490 Chomwe chinamutembenuza iye, chinali mpheta yaing’ono. Pamene . . . Ngati ine ndingalitchule . . . osati Angelo Oyera. Kodi dzina lake anali ndani, tsopano? Agadabus [Sizikudziwika ngati limalembedwa chomwecho—Mkonzi.], Agadabus Woyera, ine ndikukhulupirira ilo linali. Ine sindikutsimikiza za dzina limenelo, tsopano. Koma, mulimonse, iye anapita kumeneko, ndipo iwo anakatenga zina za izi . . .

491 Iwo anawatcha iwo angelo chifukwa, anthu ndi Asiriya ndi ena otero anali akuda mwa khungu, ndipo Azungu awa anali ndi tsitsi lalitali, loyera, lopiringizika, mutu wa bulondi, Angelezi-Achisaxoni, inu mukudziwa, a maso a buluu. Ndipo iwo anati, “Iwo ankawoneka ngati Angelo,” ndipo chotero iwo analitcha ilo “Dziko la Angelo.”

492 Ndipo—wantchito wa Ambuye anapita uko ndipo anali kulalikira kwa mfumu yawo, ndipo iwo anali atakhala pa malo aakulu, amoto otseguka. Ine ndinali kuwerenga mbiriyakale ya izo si kale litali. Ndipo mbalame yaing’ono inawulukira mu kuwala ndipo inapita mobwerera kunjja, ndipo mfumu inafunsa funso, “Kodi iyo inachokera kuti ndipo kodi yapita kuti?” Mwaona? “Iyo inabwera mu kuwala, ndipo ife tinaiwona iyo, ndipo iyo inabwerera mu mdima momwe. Kodi umo si momwe munthu amayendera?” iye anati.

493 “Koma kodi iyo inali chiani poyamba iyo isanabwere mkati muno?” anatero mlaliki, mwaona. Izo zinamugwira mfumuyo; ndipo mmawa wotsatira, iye ndi amnyumba yake anabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu. Ndiko kulondola.

494 Ndiye chiani? Munthu woyamba yemwe anayamba wakonkhedwapo kapena anayamba wabatizidwapo mwanjira iliyonse mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” anali mu mpingo wa Katolika. Kukonkha koyamba komwe kunayamba kwachitikapo, kunali mu mpingo wa Katolika. Kutsanulira koyamba komwe kunayamba kwachitikapo, kunali mu mpingo wa Katolika. Mpingo wa protestanti nthawizonse unkatatiza . . . mu Baibulo, atumwi, mwa kumiza mu Dzina la Yesu Khristu. Kulikonse. Mungopeza malo amodzi pamene iwo anali ndi china chirichonse, onani.

495 Tsopano, mu izi, nthawi yaikulu iyi, Ayuda sangakhoze . . . Ine ndinamufunsa rabbi uja, ine ndinati, “Rabbi, kodi izo zingakhale zovuta kuti inu muwakhulupirire aneneri?”

496 Iye anati, “Ine ndimawakhulupirira aneneri.”

497 Ine ndinati, “Mu Yesaya 9:6, kodi iye ankanthauza chiani, ‘Kwa ife mwana wamwamuna wabadwa?’ Kodi iye ankayankhula za ndani?”

498 Iye anati, “Iye ankayankhula za Mesiya.”

499 Ine ndinati, “Ndiye Mesiya akanati adzabadwe?”

500 “Inde, Iye akanati adzabadwe.”

501 Ine ndinati, “Ndiye ngati iye ali woti adzabadwe, iye ali . . . iye akanadzakhala nawo amake.”

502 “Inde, iye akanayenera kudzakhala ndi amake. Ndipo Iye akanayenera kudzakhala ndi abambo, naponso,” iye anatero.

503 Ine ndinati, “Mwamtheradi. Ndipo kodi izo zingakhale zovuta kuti inu mukhulupirire kuti uyo akanakhala ali . . . kuti Mulungu Yehova Wamkulu yemwe anatsegula Nyanja Yofiira, sakanakhoza kubala mwana uyu mwa kubala kwachiyero?” Mwaona? Apo iye anali.

504 Iye anati, “Koma inu simungakhoze kumupanga Iye amulungu atatu.”

505 Ine ndinati, “Iye si amulungu atatu.” Ine ndinati, “Ndi ubale wanji womwe Mesiya ati adzakhale kwa Mulungu?”

506 Iye anati, “Iye adzakhala ali Mulungu.”

507 Ine ndinati, “Tsopano inu mwazimvetsa izo. Tsopano inu mwazimvetsa izo, Iye ndi Mulungu.” Ndi izo ndendende.

508 Ndiye iye anayesera kundiuza ine, anati, “Chabwino, munthu uyu anali wakuba, Yesu waku Nazareti uyu. Iye anali wakuba.”

509 Ine ndinati, “Rabbi, Iye anali wakuba motani?”

510 “Chabwino,” iye anati, “malemba anu omwe ananena kuti ‘Iye anapita mmunda wa chimanga pa tsiku Lasabata, ndipo anakatengamo chimanga.’”

511 Ine ndinati, “Tsopano, rabbi, inu mukudziwa bwinoko . . . zochuluka za Malemba kuposa izo. Malemba anu omwe amanena kuti izo nzololedwa, ‘Ndi mwamalamulo kuti munthu apite ndi kukadya chimanga chochuluka monga momwe iye akufunira, koma asachiike icho mu thumba lake ndi kuchinyamula icho.’ Lamulo lanu lomwe, rabbi.”

512 Ndipo iye anaima apo pang’ono pokha, i—i—iye anazikhulupirira izo, chifukwa i—iye anachitira umboni. Iye anati, patapita kanthawi, “Chabwino, n—nchiani chinapangitsa maso a John . . .” Anati, “Kodi iwe unazichita motani izo?”

513 Ine ndinati, “Mu Dzina la Yesu Khristu.”

514 “Anha.” I—iye sankadziwa; anati, “Chabwino, inu simungakhoze kumudula Mulungu mu nthuli zitatu.”

515 Ine ndinati, “Iye anali Yehova atawonetseredwa mu thupi, rabbi. N . . . Ndicho chomwe Iye anali, Iye anali Yehova mu thupi. Dzina lake lomwe la umunthu, ilo linali Dzina la chiwombolo, chifukwa palibe dzina lina linapatsidwa pansu pa Kumwamba lomwe munthu angakhoze kupulumutsidwa nalo, kokha kupyolera mu Dzina laumunthu la chiwombolo ilo: Ambuye Yesu Khristu. Ndiko kulondola. Iye anali Mulungu, Iye ndi Mulungu, Iye nthawizonse adzakhala ali Mulungu, ndizo ndendende kulondola, Ambuye Yesu Khristu.”

516 Tsopano, ine ndikukhulupirira kuti mpingo wa Amitundu utero posachedwapa . . . kutsirizitsa kwa thupi la mpingo wa Amitundu. Zitseko zapakati . . . Yesu anatero, mu Mateyu 24, (Ine nditenga Lemba limodzi ilo kwa miniti), Iye anati, “Iwo adzapondereza pa makoma a Yerusalemu mpaka nyengo ya Amitundu idzatsirizidwe.”

517 Tsopano penyani. Izo zinaperekedwa ndi Ambuye wathu Yesu, mu Mateyu 24, kuti Ayuda akanati adzachotsedwe pa chithunzipo. Daniele anatero, mmbuyo umo mwa aneneri akale, iye ananena kuti ‘padzakhala pali sabata la sevente loyikidwa apobe, kwa Ayuda. Ndipo Mesiya akanadzabwera (Kalonga) ndi kudzanenera mkati mwa sabata la sevente, zomwe zinali zaka seveni, iye akanadzadulidwa pakati pake. Taonani momwe izo zinaliri zangwirowo, Yesu analalikira ndendende zaka zitatu ndi theka ndipo anapachikidwa. Koma pali zitatu . . . Izo zinabwera kumene pa funso lina ili apa. Pali zaka zitatu ndi theka zaikidwabe kwa iwo, kwa Ayuda. Izo ziyenera kukhala.

518 Tsopano ngati inu mutatenga Chivumbulutso, mutu wa 7, Yohane anawona Ayuda handiredi ndi forte foro sauzande akusindikizidwa, a mafuko thwelofu a Israeli. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Apabe kale zoti zichitike, zobwera mtsogolo.

519 Tsopano taonani momwe ziriri zokongola, ife tisanatseke tsopano. Penyani mo—momwe izo zikuzungulirira. Tsopano, Ayuda awo achititsidwa chidima.

520 Tsopano, Ayuda awa apa, ambiri a iwo kuno, ali basi. . .inu mukudziwa momwe iwo aliri, iwo agwirizira chuma cha mdziko. Ndipo iwo ali basi—anthu a ndalama basi, ndipo ndizo zonse zomwe inu mungapange pa izo, mwaona; ndi amwano kwambiri, ndi osayanjanitsika, ndipo sangamvetsere. Koma, awo si omwe Iye anali kuwakamba, ngati inu mungazindikire.

521 Tsopano, Amitundu. . .Tsopano penyani, kwatsalira panobe zaka zitatu ndi theka kwa Ayuda awa. Tsopano, Yesu ananena kuti mzinda wa Yerusalemu uzidzappededwa ndi Amitundu mpaka nyengo ya Amitundu. . .(Tsopano, inu anthu omwe simumakhulupirira mu nyengo, nanga bwanji izo?) . . .Mpaka nyengo ya Amitundu idzakhale itatha. Ndipo pamene nyengo ya Amitundu idzatha (nthawi ya Amitundu idzatha), ndiye mzinda udzaperekedwanso kwa Ayuda. Ndipo Yesu anapitirira kunena kuti kam’badwo. . .Anati, “Pamene inu mupita kunja ndi kuuwona mtengo wa mkuyu ukuyamba kuphuka, ndi mitengo ina yonse ikuphuka,” anati, “inu mumadziwa kuti chirimwe chayandikira.” Anati, “Chomwechonso pamene inu mudzawona zinthu izi zikuchitika, mudzadziwe kuti nthawi yayandikira, pa khomo; ndipo indetu ine ndikuti kwa inu kuti kam’badwo kameneka sikadzatha mpaka zinthu izi zitakwaniritsidwa.”

522 Tsopano, iwo ankayembekezera izo mu kam’badwo ako, “Ndi chomwe Iye anali kuchikamba.” Sichoncho konse!

523 Mvetserani! Iye anati, “Kam’badwo komwe kadzawona mtengo wa mkuyu ukuyamba kuphuka.” Tsopano penyani, Iye anati, “Mtengo wa mkuyu, ndi mitengo ina yonse.” Tsopano, mwa kuankhula kwina, “Kudzakhala kuli chitsitsimutso cha konsekonse pa nthawiyo.” Tsopano penyani ulosi uwu, momwe iwo ukugwirira ntchito umu ndi kungolumikizanira umo mwanngwiro. Tsopano penyani. “Mitengo ina yonse ikuyamba kuphuka, kutsitsimuka.” Mtengo, pamene iwo uyamba kuphukira, iwo ukutsitsimuka. Ndi kulondola uko? Tsopano, aliyense akudziwa, mphunzitsi wauneneri, kuti mtengo wa mkuyu nthawizonse wakhala uli Myuda. Ife tikudziwa izo. Ndi Myuda. Tsopano. . .

524 Ndipo tayang’anani pa Yoweli, pamene iye anazitenga izo, iye anati, “Zomwe chimbalanga chinasiya, chirimamine anadya; zomwe chirimamine anasiya, dzombe linachidya; ndipo zomwe dzombe linadya. . .” Ngati inu mungazindikire, ndi kachiroombo komwe komweko, kusintha, kosiyana: chimbalanga, chirimamine, ndi dzombe. Zonsezo ndi kachilombo komweko, kungokhala kusintha kosiyana kwa moyo wake. Tsopano penyani, kachilombo komweko kanayamba kudya pa mtengo wa Chiyuda uwo kumbuyo uko chinaudula iwo, ndipo icho chinayamba kuodya ndi kuodya ndi kuodya mpaka unafika

ku chitsa; komano iye anati, “ ‘Ine ndidzabwezeretsa,’ atero Ambuye, ‘zaka zonse zomwe chimbalanga chinaudya iwo. Ndipo ine ndidzawapanga anthu anga chisangalalo.’” Mwaona? Tsopano, mtengo wakhala ukudyedwa mpaka pansi. Amitundu anamezanitsidwa mwa iwo, izo nzoona. Chabwino, ife tiyenera kubala chipatso.

⁵²⁵ Tsopano pamene nthawi yamapeto ibwera, pamene ife tizifika kumapeto (ngati ine ndikuziwona izo molondola), Uthenga uli: pakuyenera kukhala pali chitsitsimutso chachikulu chikuchitika.

⁵²⁶ Tsopano, kodi inu mumadziwa kuti mbendera ya Chiyuda ndi mbendera yakale kwambiri mu dziko? Ndipo iyo yakhala ili matalala kwa zaka thuu sauzande, kuposa izo, pafupi zaka twente faifi handiredi. Mbendera ya Chiyuda, nyenyezi ya nsonga sikisi ija ya Davide, siimawuluka kwa zaka twente-faifi handiredi; kuyambira pa kutengedwera k—ku Babeloni. Ndipo tsopano, chifukwa Ufumu wa Chiroma unawatengera iwo uko (ndipo Mesiya anabwera ndipo iwo anamukana Iye), ndipo anamwazikanira ku mphepo zinai za dziko lapansi. Koma kodi inu mumadziwa, pa Meyi 6, 1946, mbendera iyo inabwereranso ku Yerusalemu kachiwiri? Kodi inu mumadziwa, pa Meyi 7, 1946, Mngelo wa Ambuye anawonekera kwa ine (tsiku lotsatira) kuno, ndipo anandituma ine ku dziko lonse kuti ndikabweretseko chitsitsimutso? Mmawa wotsatira womwe! Pamene mbendera iyo inakwezedwa mu Yerusalemu, pa kulowa kwa dzuwa madzulo amenewo, Mngelo wa Ambuye anawonekera kuno mu United States pa nthawi yomweyo. “Pamene inu mudzawona mtengo wa mkuyu ndi mitengo ina yonse ikuphuka!”

⁵²⁷ Ndi angati akukumbukira Nyenyezi itapachikika motsika kuno ku Mtsinjwa wa Ohio, zaka zambiri zapitazo, pamene Iye anati . . . Ndi ichi chithunzi Chake pano apabe, pamene Iye anali kubwera pansi. Anati, “Uthenga wako udzapita patsogolo ngati wotsogolera kudza kwachiwiri, basi monga Yohane anapita patsogolo monga wotsogolera kudza koyamba.” Ndipo, taonani, kuzungulira dziko kwasesa chitsitsimutso. Makumi a zikwi kuchulukitsa ka zikwi ndi zikwi, ndi chitsitsimutso chachikulu.

⁵²⁸ Onse azamalamulo, ndi onse osiyana kuzungulira dziko, ndi mipingo yaikulu inati, “Masiku a Billy Sunday anatha.” Koma pamene iwo anawuona mpingo ukuyamba kutsitsimuka (anthu wamba), iwo anasowa kubisa nkhope zawo. Charles Fuller bwezi atawatenga malowo, koma iye anali atakalamba kwambiri; kotero iwo anapita ndi Billy Graham. Ndipo Mulungu anamutenga Billy Graham . . . kapena mpingo wa Baptisti unatero, ndipo iwo onse anabwera momuzungulira iye. Ndipo Billy Graham si mlaliki watheka kuposa momwe M’bale Neville ali, pokamba za kukhala mlaliki, osati a . . . ayi, mwanjira iliyonse ayi. Koma ndi chiani icho? Iwo ankayenera kuti achite izo, ndi mwabungwe, ndipo aliyense anapita

mozungulira izo, kusunkhana momuzungulira. Billy amanena chinthu chomwecho. Mwaona, iwo ankayenera kuti achite izo. Ndipo izo zinkayenera kuti zichitidwe kuti akwaniritse Mawu a Mulungu. Iwo analibe Mzimu woti awusonkhanire mouzungulira, kotero iwo ankayenera kutenga Mawu kuti azisonkhanira mowazungulira; chotere iwo amatero. Ndipo Billy ndi mlaliki wa Mawu, ndi wokonedwa, ndipo iwo amasonkhana momuzungulira; chotero izo zinaika onse ozizira a mwachizolowezi mu kusunkhana kwawoko. Ndipo Chinthu chazimu, ndi machiritso Auzimu, ndi mphamvu ndi magwiridwe antchito ndi zina zotero, mwa zozizwitsa za Mulungu, kuwuika uwu. . . Mpingo, Mkwatibwi wokwatulidwa yemwe ali ndi mafuta mu nyali Yake, kumuika Iye mu chitsitsimutso. Mwaona? Ndipo mpingo wachizolowezi wozizira unali ndi chitsitsimutso chake. Ndipo pano pali Israeli akutembenuka ndi chitsitsimutso chawo.

⁵²⁹ Ine ndiri nayo filimu ku nyumba yanga uko pakali pano, *Maminiti Atatu Pasanafike Pakati pa Usiku*. Ndipo ife tiri nacho chithunzi cha Ayuda amenewo akubwera umo. Akubwera umo; inu munachiwona icho mu magazini ya *Look*. Ndipo ngalawa, zitadzaza, zikubwera kuchokera kutali komwe ku Iran ndi kumeneko; Ayuda awo sankadziwa nkomwe kuti Yesu anali konse pa dziko lapansi, iwo anapita uko mu kutengedwera kwina kwa Babeloni. Ndizo zonse zomwe iwo ankazidziwa konse. Iwo ankalima. . . inu munaziwona izo mu magazini ya *Look* kapena *Life* ndi zinazo, momwe iwo ankalima ndi zida zakale zamitengo. Ndipo pamene iwo anaziwona ndege izo zikubwera umo, iwo anaganiza, “Izi ndizo,” chifukwa Mulungu anawauza iwo “ ‘iwo akanadzakhala ali kumeneko, ndipo akanadzanyamulidwa pobwerera ku Yerusalemu pa mapiko a mphungu.’ ” Ndiko kulondola. Uko iwo ali. Ndipo Myuda anati, “Izi ndizo.” Iwo anakwera umo, ndipo ife tiri nacho chithunzi chawo ndi mawu awo omwe, ndipo ankawafunsa iwo; akubwera kuchokera konsekonse pa dziko. Ena a iwo atanyamula achikulire awo pa nsana pawo, ndipo iwo ali akhungu ndi olumala. Ndipo iwo anali akutsika mu ngalawa kuchokera ku mbali zonse zosiyana za mdziko, akubwera umo.

⁵³⁰ Ndipo iwo anayamba kutola miyala mu matumba, kuichotsa pa nthakayo; ndipo lero iwo apeza akasupe a madzi, ilo ndi dziko laulimi kwambiri mdziko. Nyanja Yakufa ili ndi chuma chochuluka kuposa maiko ena onse ataikidwa pamodzi. Ayuda akubwerera kwao; izo zakhala zitabisika kwa Amitundu, koma iwo akuyanga ngati duwa.

⁵³¹ Iwo ananena kwa iwo—Ayuda awo, iwo anati, “Kodi inu mukubwerera kuti mudzafere mu dziko lakwanu.”

⁵³² Anati, “Ife tikubwerera kuti tidzamuwone Mesiya. Ali kuti Iye? Iye amayenera kukhala ali kuno.”

533 M'bale, pamene inu mukuuwona mtengo wa tirigu ukuyamba kuphuka, Iye anati, "M'badwo uno sudzatha mpaka zonse izi zidzakhala zitakwaniritsidwa." Tayang'anani pa chitsitsimutso ndi achizolowezi. Tayang'anani pa chitsitsimutso ndi Mpingo. Tayang'anani pa chitsitsimutso chikudza ndi Ayuda, iwo akuyembekezera kudza kwa Mesiya. Mpingo, Mpingo wodzazidwa-Mzimu, Mkwatibwi ndi...anamwali omwe ali ndi mafuta mu nyali zawo akalowa mu Mgonero wa Chikwati.

534 Ayuda adzati, "Ichi ndicho icho. Ndi uyo Mulungu wathu yemwe ife tamuyembekezera." Apo ndi pamene handiredi ndi fote-foro sauzande anu...Achiruselo aja anasokonezeka umo. Ndi awo Ayuda aja ataima uko omwe ati adzambulandire Iye. Iwo anati, "Ndi uyo Mulungu wathu yemwe ife timamuyembekezera." Iwo adzamuwona Iye, adzati, "Kodi Inu mwawatenga kuti awo? Kodi Inu munawatengera kuti mabala awo ali mu dzanja Lanu?"

535 Iye anati, "Ine ndinawatenga iwo kunyumba ya abwenzi Anga." Ndiko kulondola, "Nyumba ya abwenzi Anga."

536 Kodi Iye adzachita chiani? Mpingo wa Amitundu udzatengedwera kukalowa mu Ulemerero ndipo Mkwatibwi adzakwatiwa kwa Khristu.

537 Kodi Yosefe anadzidziwitsa chotani kwa abale ake? Iye anamuchotsapo Wamitundu aliyense pa kukhalapo kwake. Iye ndithudi anatero. Nchiani chiti chidzachitike kwa otsalira a mbewu ya mkazi? Chinjoka chinalavula madzi kuchokera mkamwa mwake kuti chipange nkondo; Yesu anati, "iwo adzaponyedwa ku mdima wakunja, ndipo uko kudzakhala kuli kulira ndi kuisima ndi kukukuta kwa mano," maora aakulu a kuzunzidwa ndi mayesero adzabwera kwa mpingo wa Amitundu.

538 Nchiani chiti chidzachitike ndiye? Pamene ofera akubwera, pamene Mulungu adzalekanitsa chirichonse kuchokera kwa Ayuda awo kumeneko, Yesu adzabwerera monga Yosefe anachitira. Pamene iwo anamumva Yosefe, pamene iye anawachotsapo omulondera ake onse ndi china chirichonse, ndipo iye anamuwona Benjamini wamng'ono ndi iwo ataima apo, ndipo anali akulapa chifukwa chomupha Yosefe. Iwo ankaganiza kuti anamupha Yosefe, ndipo apa iye anali ataima patsogolo pawo. Iye anati, "Ine ndine Yosefe. Ndine m'bale wanu."

539 Ndiye iwo ananjenjemera kwenikwenidi, "Iye ndi Yosefe. Tsopano ife tikumudziwa iye."

540 Pamene Iye ati adzati, "Ine ndine Yesu. Ine ndine Mesiya."

541 Iwo adzati, "O, mai, tsopano zomwe ife titi tizilandire!"

542 Zonsezo zinachitidwira kwa ulemerero wa Mulungu. Izo sizidzakhala Iye... Chabwino, iwo akanakhoza kumumu iye akulira kutali uko ku nyumba yachifumu ya Farao, Yosefe akuwalirira iwo.

543 Dikirani mpaka Yesu adzawawone Ayuda awo omwe anachita kuwakantha khungu kuti atilole ife Amitundu tikhale nawo mwayi wobwera umu, ilo lidzakhala ora lake, ine ndikukuuzani inu. Iye adzawatenga Ayuda amenewo, inu musati muzidandaula konse, Ayuda awo adzapulumutsidwa. Inde, bwana, uko adzayenera kukhala ali uko. Ndipo ilo ndi lingaliro langa la izo, ine sindingakhoze kuziwona izo kwina kulikonsenso mu Lemba. Inu muyenera kumawasunga ma firii awo palimodzi, kachiwiri.

544 Inu muyenera kumusunga—anamwali opusa, m—mpingo wamwadzina chabe, wongodzinenera, mwaona. Inu muyenera kumawutenga mpingo... Ndizo, Myuda poyamba, Myuda poyamba, yemwe ali munthu wochititsidwa khungu akudikirira kumzere wakumbali. Inu muyenera kuti mufike pamwamba pa sitepe yotsatira, omwe ali anamwali opusa, omwe anali kuchita mwachidodo, ndipo anangopita uko ndi mpingo, ndi kujowina mpingo, ndi kukhala munthu wabwino ndithu. Ndiye inu muyenera kuwutenga Mpingo, wauzimu, Mkwatulo, Mkwatibwi, apo iye waima. Anthu atatu awo, inu simungakhoze... iwo si osakanizikana, osati pang'ono. Iwo onse si ofanana. Osati za Amboni za Yehova zokuti “handiredi ndi forte-foro sauzande ndi mkwatibwi”; uko nkulakwitsa. Awo ndi Ayuda, mwaona. Apo pali Mkwatibwi, Ayuda, ndi anamwali opusa. Ndipo inu mukuwatenga onsewo, ndipo mukuti, “Chabwino, onsewo ndi malo atatu osiyana.” Iwo onse ndi, magulu atatu osiyana a anthu. Zedi, iwo sangakhoze.

545 Ndiye pamene Yesu akubwerera ku dziko lapansi... Ayuda, kodi iwo ndi chiani? Adindo a mkachisi. Ndipo pamene Yesu azibwerera, Iye azibwera limodzi *ndi* Mkwatibwi. Yesu akubwera nthawi zitatu: Iye anabwera nthawi yoyamba kuti *adzawuombole* Mpingo Wake, Iye akubwera nthawi yachiwiri kuti *adzaulandire* Mpingo Wake, Iye akubwera nthawi yachitatu limodzi *ndi* Mpingo Wake. Mwaona? Ndendende. Chotero konseko ndi kubwera kumodzi kwakukulu, zonsezo ndi Mulungu mmodzi wangwiro, chiwombolo chimodzi chachikulu changwiro... chirichonse; izo zikubwera mu utatu, koma zonsezo ndi Chimodzi. Mukuona? Si anthu atatu, osati zitatu *izi*; ndi Munthu mmodzi yekha, Mpingo umodzi, Thupi limodzi, Khristu mmodzi, Ambuye mmodzi “mwa inu nonse, ndi kupyolera mwa inu nonse,” ndi zina zotero monga choncho. Zonse mmodzi!

546 Ambuye akudalitseni inu. Ine ndakusungani inu motalika kwambiri.

⁵⁴⁷ Ambuye akalola, tsopano, ngati ine ndidzakwanitse kubweranso kwa mausiku angapo, kapena Lamlungu usiku kapena chinachake chonga izo, ngati abusa pano sadzakhala ndi chinachake pa mtima wawo, ine ndidzayesera kuti ndidzawayankhe awa pano. O, pali ena abwino apa. Ndi angati akufuna kuti awamve iwo? O, ine ndikungowakonda iwo. Ndiloleni ine kuti ndidutse mwa iwo kachiwiri, mofulumira kwenikweni ndithu, ife tisanapereke msonkhanowu kwa abusa.

⁵⁴⁸ Tangomvetserani kwa izi. [M'bale Branham akuyankha mafunso eyiti otsatirawa mu Gawo III, kuyambira pa paragarafu 668, ngati funso 67 kudutsa 74—Mkonzi.]:

Ndi pati pomwe miyala imai- . . . Kodi miyala iyi imaimira chiani mu Chivumbulutso 21? Ilo ndi labwino.

Fotokozani zamoyo zinai za Chivumbulutso 5. Aponso pali labwino lina.

Kodi akulu twente-foro ndi ndani? Ilo ndi labwino lina, mwaona.

Kodi chingwe chofiira cha Genesis 38 chinkatanthauza chiani? Inu kumbukirani, iye anapita ndipo anakamutenga mpongozi wake yemwe ndi kugona naye ngati hule; ndipo anapanga mtengo wake ndipo anabwererako; ndiyeno pamene mwanayo ankatulukira, iwo anaika chingwe chofiira kuzungulira dzanja lake (iye anakankhira panja ndiyeno iye anabwerera mkati), w—wotsatira anabwera patsogolo pake. O, ilo ndilo labwino; ndithudi ilo liri.

Kodi mphatsozo ndi chiani zoti zizidzatumizidwa zokhudza imfa ya mboni, mu Chivumbulutso 11? Ndi pamene Mose ndi Eliya ati adzabwerere kwa chitsitsimutso cha kwa handiredi forte-foro sauzande awa. **Kodi mphatsozo ndi chiani?** Tapenyani zomwe iwo ali, izo nzabwino.

Kodi oyera azidzakakhala kuti zikadzatha zaka chikwi chimodzi . . . (ilo ndi labwinonso la mtundu wanji, mnyamata. Ti . . .) . . . paulamuliro? Kodi iwo adzakhala ndi thupi?

Kodi ife tidzawaweruza chotani angelo?

Ndi tsitsi liti limakhala la angelo mu I Akorinto? Mu Bukhu la I Akorinto. Ndi labwino, labwino kwenikweni.

⁵⁴⁹ Ambuye akudalitseni inu. Ine ndikuyembekeza Ambuye ataloleza kuti ife tisonkhane pamodzi ndi kudzakambirana zinthu izi, zonsezo ndi za kwa ulemerero Wake. Ife tikhoza kusagwirizana pa malingaliro a iwo; koma ine ndinena chinthu chimodzi, ngati inu nonse mukupeza chisangalalo chochuluka pa kuzimva izi pamene ine ndiri kuyankhula za izo, ife tikukhala ndi nthawi yodabwitsa. Amen. Amen.

⁵⁵⁰ Chabwino, Ambuye akhale wabwino kwenikweni kwa inu tsopano. Musati muyiiwale misonkhano. Kuwulutsa kwa

M'bale Neville, tsopano, kuli pa WLRP, Loweruka mmawa naini koloko; gulu la anai la a Neville, ndipo ine ndikutsimikiza iwo adzakuchitirani inu bwino, katseguleni ndi kukamvetsera kwa iwo. Ndipo ngati ine ndingathe, ngati ine nditi ndikabwerere mu nthawi, kapena ndidzawona ngati nditi ndikabwerere, ine ndidzamuimbira mkazi wanga; ngati Ambuye andilole ine kuti ndipite ndikamuwone M'bale Bosworth wokondedwa wokalamba. I...Inu nonse...ndipo ine ndidzabwerera Lamlungu usiku.

⁵⁵¹ Ambuye akhale wabwino kwa inu tsopano. Ndipo m'bale, m'busa, bwerani kuno miniti yokha; ndipo muloleni iye atenge utumiki. Ndipo:

Musaiwale pemphero,
Yesu akakomane nanu;
Asamalira zosowa,
Pa pemphero la pabanja.

⁵⁵² Inu mumaikonda iyo? Ndi angati mumapemphera ku nyumba zanu komwe? Tiyeni tiwone, nonse...onse...Ndizo zabwino, zikhalani moyandikira ndi Mulungu. Zikhalani abwino, ana aang'ono, Mulungu azikudalitsani inu.

Chabwino, M'bale Neville.



Khalidwe Dongosolo ndi Chiphunzitso cha Mpingo, Bukhu Loyamba
(Conduct, Order And Doctrine Of The Church, Volume One)

Mauthenga awa a M'bale William Marrion Branham olalikiidwa ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito ndipo anadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Ndipo kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org